# NTCHITO YOUNIKANSO
# MALAMULO OYENDETSERA DZIKO LINO

# MAGANIZO A ANTHU PA OKHUDZA MALAMULO OFUNIKA KUWAUNIKANSO

**ZA MKATIMU**

Mawu Otsogolera

CHIGAWO CHOYAMBA

1. MAWU OYAMBA
1.1 Udindo wa bungwe la Malawi Law Commission
1.2 Bungwe loima palokha
1.3 Malipoti omwe bungwe la Malawi Law Commission latulutsa

2. NDONDOMEKO YA NTCHITO YOUNIKA MALAMULO OYENDETSERA DZIKO LINO
2.1 Kumva maganizo a anthu
2.2 Msonkhano waukulu woyamba wounikanso malamulo
2.3 Ntchito yosintha malamulo ndi msonkhano waukulu wachiwiri wounika malamulo

CHIGAWO CHACHIWIRI

MUTU 1

1. DZIKO LA MALAWI
1.1 Chiyankhulo cha mtundu wa Amalawi
1.2 Kusiyanitsa pakati pa Nthambi za Boma
1.3 Mfundo zofunikira

MUTU 2

2. UFULU WACHIBADWIDWE WA ANTHU
2.1 Chilango chonyonga
2.2 Maukwati opanda nkhoswe
2.3 Ufulu wochita ndale
2.4 Ufulu wokhala nzika ya dziko la Malawi
2.5 Ufulu woti amayi azikhala aphungu a kunyumba ya malamulo
2.6 Kugonana pakati pa akazi ndi amuna
2.7 Kugwira munthu womuganizira kuti waphwanya malamulo ndi kumuzenga milandu mwachilungamo
2.8 Ufulu wa maphunziro
2.9 Ufulu wa achinyamata
2.10 Msinkhu woyenera kuti munthu alowe m'banja
2.11 Ufulu wa ana
2.12 Ufulu wosasankhana
2.13 Ufulu wa pantchito
2.14 Kuchita zinthu mwachilungamo

MUTU 3

3 NTHAMBI YA BOMA YOPANGA MALAMULO
- 3.1 Seneti
- 3.2 Kuchotsa phungu wa kunyumba ya malamulo pampando
- 3.3 Phungu wochoka mchipani chake nkukalowa chipani china chomwenso chili ndi aphungu mnyumba ya mamalulo
- 3.4 Nthawi yokhala pampando wa phungu wa kunyumba ya malamulo
- 3.5 Zomuyenereza munthu kukhala phungu
- 3.6 Aphungu ogwira ntchito mophatikiza ngati nduna
- 3.7 Sipikala wa kunyumba ya malamulo
- 3.8 Zina ndi zina
  - 3.8.1 Aphungu kudulira chisamani nyumba ya malamulo
  - 3.8.2 Kuitanitsa msonkhano wa Aphungu

MUTU 4

4 CHISANKHO
- 4.1 Bungwe Loyendetsa chisankho
  - 4.1.1 Wapampando wa Bungwe Loyendetsa chisankho
  - 4.1.2 Anthu oyenera kusankhidwa kukhala m'bungwe loyendetsa chisankho
  - 4.1.3 Ntchito za bunbwe loyendetsa chisankho
- 4.2 Mitundu ya chsankho
  - 4.2.1 Kukchuluka kwa anthu osankha pulezidenti
  - 4.2.2 Njira yosankhira aphungu a kunyumba ya malamulo
  - 4.2.3 Chisankho cha pulezidenti ndi aphungu
  - 4.2.4 Nthawi yolengezera zotsatira za chisankho
  - 4.2.5 Oyenera kuponya voti
  - 4.2.6 Chisankho chapadera
- 4.3 Zina ndi zina
  - 4.3.1 Kuunikanso malamulo oyendetsera chisankho

MUTU 5

5 NTHAMBI YA BOMA YOLAMULA
- 5.1 Kulumbiritsa Pulezidenti kapena wachiwiri wake
- 5.2 Zomuyenereza munthu kukhala pulezidenti kapena wachiwiri kwa pulezidenti
- 5.3 Ofesi ya Wachiwiri woyamba kwa pulezidenti
- 5.4 Ofesi ya wachiwiri kwa wachiwiri kwa pulezidenti
- 5.5 Kuchuluka kwa nduna za Boma
- 5.6 Zina ndi zina
  - 5.6.1 Nthawi yoyenera kuti pulezidenti kapena wachiwiri wake akhale pampando
  - 5.6.2 Ndondomeko zochotsera pulezidenti kapena wachiwiri wake pampando
  - 5.6.3 Kusamala/kuyang'anira pulezidenti kapena wachiwiri kwa pulezidenti amene wachotsedwa pampando
  - 5.6.4 Pulezidenti kusintha zipani
  - 5.6.5 Kupatsirana mpando wa pulezidenti motsata zigawo za dziko

MUTU 6

6 NTHAMBI YA BOMA YOWERUZA
6.1 Msinkhu wopumira pa ntchito Majaji
6.2 Msinkhu woyenera woti munthu atha kusankhidwa kukhala Jaji
6.3 Wachiwiri kwa Wamkulu wa Majaji
6.4 Ofesi yoona za malamulo
6.5 Bungwe Loona za anthu Ogwira ntchito za malamulo
6.6 Kusankha Majaji
6.7 Kuchotsa Majaji pampando
6.8 Khoti Lounika malamulo
6.9 Khothi lomva madandaulo a anthu ogwira ntchito
6.10 Zina ndi zina
6.10.1 Malipiro a wamkulu wa majaji
6.10.2 Ndalama zoyendetsera ntchito za makhothi

MUTU 7

7 MABUNGWE OKHAZIKITSIDWA NDI MALAMULO OYENDETSERA DZIKO LINO

7.1 Bungwe Loona za Ufulu wa chbadwidwe wa anthu (Malwi Human Rights Commission)
7.2 Ofesi ya Mkulu womva madandaulo a anthu (Ombudsman)

MUTU 8

8 MABUNGWE ENA
8.1 Komiti yoona za Chitetezo Mdziko
8.2 Dipatiment ya Boma yoona za anthu lolwa ndi kutuluka mdziko muno
8.3 Bungwe lolimbana ndi mchitidwe wa ziphuphu
8.4 Banki Lalikulu la Boma
8.5 Bungwe Loona za anthu ogwira ntchito za Boma
8.6 Apolisi
8.7 Bungwe la mafumu

MUTU 9

9 ZINA NDI ZINA
9.1 Kuvomereza ndi kusainira malamulo okhudza maiko a padziko lapansi
9.2 Ofesi ya Mkulu wolangiza Boma pa za malamulo
9.3 Kuulula chuma potenga mpando wosankhidwa
9.4 Kufunika kwa ntchito younikanso malamulo
9.5 Kayendetsedwe ka ntchito za chuma
9.6 Nyumba ya malamulo ya ana

## MAWU OTSOGOLERA

Mbuku lino muli maganizo a anthu ndi magulu a osiyanasiyana omwe Bungwe Loona Za Malamulo a dziko lino la Malawi Law Commission lidalandira kuchokera mwezi wa Okutobala m'chaka cha 2004 mpaka mwezi wa May 2005. Bukuli lalelembedwanso kuchokera pa maganizo a magulu osiyanasiyana a anthu omwe bugwe la Law Commission lidakomana nawo kuti limve maganizo awo pa malamulo oyendetsera dziko lino potsata zomwe bungwe la Nduna za Boma lidalamula kuti Bungweli liyende dziko lonse ndi kukumana ndi anthu ndi magulu osiyanasiyana omwe sangathe kulemba kalata ku Bungweli kuti limve maganizo awo pofuna kuonetsettsa kuti aliyense watengapo mbali pa ntchito yokonzanzo malamulo oyendetsera dziko lino.

Choncho anthu ogwira ntchito ku Bungwe la Malawi Law Commission adakumana ndi anthu oyimira zipani za ndale zosiyanasiyana zomwe zili ndi aphungu mnyumba ya malamulo ngakhalenso zomwe zilibe, mafumu ochokera mzigawo zonse zitatu za dziko la Malawi, mabungwe omwe si a boma kuphatikizapo omwe amagwira ntchito zolimbikitsa ufulu wachibadwidwe wa anthu, achinyamata komanso ana, aphunzitsi a ku sukulu za ukachenjede ndi ukadaulo (ma yunivesite), mabungwe ogwira ntchito zaluso, Bungwe la Aphungu aakazi, Alembi ndi akuluiakulu a Maunduna, madipatimenti ndi Mabungw a Boma, Oweruza milandu komaso nduna za Boma.

Tsono Buku lino laika pamodzi maganizo a magulu amaenewa potsata mfundo komanso mafunso omwe iwo adapereka. Maganizo omwe anthu adapereka pa misonkhano yosiyanasiyana yofuna kumva maganizo awo. Bungwe la Law Commission likukhulupirira kuti maganizo omwe ali m'buku lino athandiza kukumbutsa anthu pa m fundo zoyenera kukambirana pa Msonkhano Wounikanso Malamulo Oyendetsera Dziko Lino.

Bukhuli lili m'zigawo ziwiri. M'chigawo loyamba muli maganizo a anthu ndi mabungwe asiyanasiyana pa ndondomeko ya ntchito younikanso malamulo a dziko. Chigawo chachiwiri chikufotokoza maganizo a anthu ndi magulu osiyanasiyana pa za magawo ndime za m'Malamulo Oyendetsera dziko lino zoyenera kuziunikanso.

Bukuli lalembedwa ndi Mayi Janet Laura Chikaya yemwe ndi Mkulu Woona Zosintha Malamulo ku Bungwe la Malawi Law Commission.

## CHIGAWO CHOYAMBA

## 1. MAWU OYAMBA

### 1.1 Undindo wa bungwe la Malawi Law Commission

Bungwe Loona za Malamulo m'dziko muno la Malawi Law Commission lidakhazikitsidwa kudzera Mgawo XII la Malamulo Oyendetsera Dziko Lino ndipo lili ndi mphamvu komanso udindo wounika ndi kusintha malamulo a dziko la Malawi kuti azigwirizana ndi Malamulo Oyendetsera Dziko Lino komanso malamulo ena a maiko ndi mabungwe a kunja omwe amakhudza dziko lino. Bungweli lilinso ndi undindo ndi mphamvu lounika ndi kupereka maganizo ake pa mfundo kapena china chilichonse chokhudza malamulo Oyendetsera dziko Lino. Bungwe la Law commission lili ndi mphamvu yolandira maganizo okhudza malamulo a dziko lino kuchokera kwa m'Malawi aliyense kapena bungwe kapenanso gulu lina lililonse ndipo ilo liyenera kuchita kafukufuku ndi kupereka lipoti la zomwe lapeza kwa Nduna ya Za Chilungamo yomwenso imayenera kukapewreka lipotilo Kunyumba ya Malamulo.

Mkulu Woona za Malamulo (Law Commissioner) ndiye wamkulu wa Bungwe la law Commission ndipo amasankhidwa ndi Pulezidenti wa dziko, atayenerezedwa ndi bungwe loona za anthu ogwira ntchito za makhothi (Judicial Service Commission).

Mkuluyu mogwirizana ndi Bungwe Loona za anthu Ogwira ntchito za makhothi (Judicial Service Commission) amasankha akatswiri oti azithandizana nawo ntchito kuti cholinga chomwe

bungweli lidakhazikitsidwira chikwaniritsidwe. Akatswiriwa amasankhidwa motsata ntchito yomwe ilipo, luso lawo malamulo omwe akuunikidwawo kapenaso pa malamulo ena omwe akukhudzana ndi malamulo omwe akuunikidwawo ndipo ndipo nthawi yokhala pantchitoyi imatengera kukula kwa ntchitoyo.

## 1.2 Bungwe loima palokha

Bungwe la Malawi Law Commission lidakhazikitsidwa ngati bungwe la Boma loima palokha kuti lizigwira tnchito zake mwaufulu opanda munthu wina kapena bungwelina lililonse kulilamulira kapena kulisokoneza, mogwirizana ndi ndime 136 ya Malamulo Oyendetsera Dziko Lilno yomwe imati:

*Bungwe Loona za Malamulo (Law Commission) lidzagwira ntchito zake maufulu popanda munthu wina kapena bugwe lina lililonse kulilamulira kapena kulisokoneza.*

## 1.3 Malipoti Omwe Bungwe la Malawi Law Commission latulutsapo

Chiyambire ntchito zake m'chaka cha 1996, bungwe la Malawi Law Commission latulutsapo malipoti khumi ndi atatu. Malipotiwa ali motere:

Lipoti lokhudza kuunikanso malamulo ena okhudza kugwirira mwana wamn'gono, Ukwati, Anthu okhala nawo ndi nzika za dziko lino la 1996
Lipoti lokhudza kuunikanso malamulo oyendetsera dziko lino la 1998
Lipoti lokhudza ndondomeko zoperekera belo la 2000
Lipoti lokhudza kuunikanso Malamulo a Dziko lino la 2000
Lipoti lokhudza kuunokanso Lamulo La Gulu la Asilikali a Nkhondo la 2001
Lipoti lokhudza kuunikanso Lakhudza Makanema, Mabuku ndi zinthu zina zosangalatsa la 2001
Lipoti lokhudza lamulo Lokhudza maphunziro komanso anthu ogwira nthcito za malamulo la 2002
Lipoti lokhudza kuunikanso Lamulo Lokhudza Mchitidwe wa Ziphuphu la 2002
Lipoti lokhudza Lamulo la Apolisi la 2002
Lipoti lokhudza kuunikanso ndondomeko zozengera milando ndi kuperka umboni mkhothi la 2004
Lipoti lokhudza kuunikanso Lamulo Lokhudza chindapusa chomwe akhothi amalamula munthu wopezeka ndi wolakwa pamlandu la 2004
Lipoti lokhudza kuunikanso Lamulo lokhudza Chuma Chamasiye la 2004
Lipoti lokhudza kuunikanso Lamulo Lokhudza Bungwe la boma loimira anthu pa milandu la 2005

Malipoti onsewa anali ndi mabilo omwe ena mwa iwo nyumba ya malamulo idawavomereza kukhala malamulo. Pakali pano bungweli likutsiriza kusindikiza malipoti ena anayi. Awa ndi Lipotiwa lokhudza kuunikanso malamulo okhudza ufulu wa chibadwiwe wa ana, Lipoti lokhudza kuunikanso Lamulo Lokhudza makhuti a Miyambo, Lipoti lokhudza Kuunikanso malamulo okhudza Kumanga maukwati ndi kusudulana kapena kutha kwa maukwati ndi Lipoti lokhudza kuunikanso malamulo okhudza malo.

## 2. NDONDOMEKO ZA NTCHITO YOUNIKA MALAMULO OYENDETSERA DZIKO LINO

Ndondomeko yomwe bungwe la Malawi Law Commission lidakonza poyamba lokhundza ntchito younka malamulo oyendetsera dziko lino idali yoti poyamba bungweli lidzaunika di kupeza zovuta zomwe zili m'malamulowa, kenaka kumva maganizo a anthu ndi magulu osiyanasiyana pa zovutazi, kuchititsa msonkhano wa dziko lonse wouniukanso malamulo a dziko linowa ndipo pomalizira ndipo kenaka bungwe lapadera lounika malamulo lomwe ndi la akatswiri a za malamulo, ndi anthu ena okhudzidwa ndi za malamulo, idzasintha malamulowo mogwirizana ndi zomwe anthu anthu adagwirizana ku msonkhano wounika malamulowo.

Koma potsata zomwe bungwe a nduna za Boma lidalamula, bungweli lidasintha ndondomekoyi kuti Amalawi ambiri atenge nawo mbali pa ntchito younikanso malamulowo. Ndondomeko yatsopanoyo idali m'dime zitatu izi:

a) Ndime yoyamba: Kumva maganizo a anthu pa misonkhano yapadera komanso kudzera m'makalata
b) Ndime yachiwiri: Msonkhano Woyamba wa Dziko lonse wounikanso malamulo a dziko lino
c) Ndime yachitatu: Kusintha malamulo mogwirizana ndi zomwe nthumwi zidagwirizana kenaka Msonkhano wachiwiri wa dziko lonse wouniknso malamulo omwe asinthidwawo

### 2.1 Kumva maganizo a anthu

Cholinga cha ndime imeneyi chinali kupatsa mwayi Amalawi kti apereke maganizo awo pa magawo ndi ndime zomwe akuona kuti sizili bwino m'Malamulo Oyendetsera Dziko lino. Bungwe la Law Commission silimaumiriza anthu kuti apereke maganizo ofanana ndi omwe anthu ena adapereka pa msokhnano wonga womwewu kwina. Cholinga chinanso chinali choti magulu makamaka zipani za ndale komanso magulu ena azidzikhulupirira kuti alindi mphamvu yotha kusintha malamulo a dziko. Pachifukwa chimenechi. Choncho bungwe la Law Commission lidaonetsetsa kuti pa zokambirana za mtunduwu

bungweli lizingomvera zomwe anthu azinena ndipo anthu adapatsidwa mwawi woyankhula zakukhosi momwe akadathera.

M’ndime imeneyi bungwe la Law Commission lidakambirana mwapaderapadera ndi nthumwi za zipani za ndale zome zili ndi aphungu m’nyumba ya malamulo, makamaka zipani za MCP, PPM, MGODE, RP ndi DPP. Bungweli lidachititsanso misonkhano yamtunduwu ndi mabungwe omwe akulimbikitsa za ufulu wachibadwidwe wa anthu, mafumu ochokera mzigawo zones zitatu za dziko lino, aphunzitsi a ku Yuninesite ya Malawi ndi Mzuzu, makampani, baungwe a mipingo, mabungwe oimira and andi achinyamata komanso atolankhani.

Bungwe la Law Commission lidakambirananso ndi bungwe la aphungu achizimayi, Alembi ndi Akuluakulu a maunduna, Madipatimenti and Makampani kapena mabungwe a Boma, akuluakulu odziwa za malamulo, komanso nduna za Boma zingapo kuimirira nthambi ya Boma yolamula.

Pa zokamiranazo maganizo osiyanasiyana nthumwi zidapereka maganizo osiyanasiyana okhudza momwe nthito yomva maganizo a anthu akadayendera. Zipani za ndale sidatsimikiza kufunika koti mafumu aikepo amaganizo awo pa ntchito yosintha malamulo oyendetsera dziko lino kuti ntchito yonseyi ikhale yovomerezeka malinga nkuti iwo ndi amene amakhala ndi anthu omwe malamulowo akuwakhudza.

Zipani zina zidati sibwino kutenga maganizo a aphungu a kunyumba ya malamulo ngati maganizo a anthu a m’madera awo chifukwa chakuti anthu m’madera ambiri masiku anu akudandaula kuti aphungu awo akunyumba ya malamulo safunsa anthu awo pa nkhani zokhudza kayendetdwe ka dziko chonsecho akachita zinthu amanamizira kuti zomwe achita kapena kulankhula ndi zomwe anthu anawatuma.

Choncho atsogoleri a zipani za ndale m’midzi ndi amene angafotokoze maganizo a anthu osati phungu nomwe amangochita zinthu potsata zomwe atsogoleri a zipani zawo alamula kapena akufuna. Maganizo enaso adali oti msonkhano ina ikachitikire m’madera momwe aphungu amaimira ndipo aphungu oimira m’maderamo akaitanidwe kuti akakhale nawo pa zokambiranazo ncholinga choti aphunguwo akavomereze ngati patafunika kuti malamulo ena absinthe malingana ndi zomwe anthu adanena. Bungweli lidalangizidwanso kuti lisankhe mfundo kapena malamulo okakambirana ndi anthu.

Kumbali yawo, mafumu adafotokoza kuti nthcito yosintha malamulo ikadzayamba, mpofunika kuti zokamirana zidzayambire m’madera omwe mafumu aakulu (ma TA) amalamilira kudzera m’makomiti a za chitukuko m’madera

(ADCs). Iwo adati zimenezi zikadathandiza kuti anthu wamba ambiri m'madera a m'midzi atange anawo mbali pa ntchito younikanso malamuloyi chifukwa Aphungu a kunyumba ya malamulo, makhansala, mabungwe omwe si a boma, ogwira ntchito za boma, magulupu ndi atsogoleri a zipani za ndale ndi mamembala a makomiti a za chitukuko m'madera. Kuonjezera apo ,mafumuwa adati ma ADC amapezeka m'dera lililonse la TA. Iwo adatinso sibwino kudalira maganizo a mabungwe si a boma chifukwa ena mwa mwa mabungwewa amachita zinthu pofuna kukwaniritsa zolinga za zipani zawo zandale kapena mabungwe amene amawapatsa ndalama zogwirira ntchito zawo.

Mafumuwo adafotokozanso kuti padafunika patakhala msoknhano wa mafumu onse m'Malawi muno kuti adzakhale ndi mwayi wopereka maganizo awo okhudza malamulo Oyendetsera Dziko lino. Koma iwo adati ngati zi sizingatheke chifukwa cha kusowa ndalama komanso nthawi, nkofunika kuti bungweli lidzachititse misonkhano ya mafumu m'boma lililonse kome Ta aliyense kapena womuimira wake adzakhaleko. Mafumuwa adagwirizananso kuti TA aliyense adzatumize nthumi khumi (10) zomwe zina mwa izo zikadakhala mabungwe omwe si aboma, amipingo komanso anthu eni ake. Mafumuwa adagwirizananso kuti amayi akahalemonso ochuluka m'gulu la nthumwizi.

Mafumuwo adafotokozanso kuti mafumu amayenera kudziwitsidwa nthawi yabwino za misonkhanoyi kuti akonzekere mokwanira. Choncho mafumuwa anati ndi bwino bungwe la Law Commission litamatumiziratu mafunso kwa mafumuwo oti azikawaganizira ndi kukambirana ndi anthu awo tsiku ka msonkhano lisadafike.

Koma bungwe la Law Commission mogwirizana ndi aYunivesite ya Malawi idaona kuti ndi bwino kuti zokambiranazi zikhudze magulu atatu a anthu motere: Atsogoleri a ndale gati gulu limodzi, anthu wamba, mabungwe omwe si aboma ndi mabungwe a mipingo ngati gulu lina, ndi anthu owira ntchito za padera ngati gulu linanso. Bungweli lidaonanso kuti ndibwino kuti pa zokambiranazo anthu azikayamba aphunzitsidwa za malamulo oyendetsera dziko lino kuti azikapereka maganizo awo akuzindikira zomwe akunena.

Bungwe la Law Commission lidagaizanso zokhazikitsiratu Bungwe lapadera Lounika Malamulowa kuti liyambiretu ntchito Msonkhano waukulu usanachitike kuti Likadzimvere lokha zomwe nthumwi zizikakambirana kumsonkhanowo. Koma bungweli adalilangiza kuti likaganizire bwino nthawi yoyenera katulutsa lipoti lokhudza msonkhanowo malinga ndi mavuto a zandale omwe ali m'dziko muno.

Mabungwe oimira ana ndi achinyamata zokambirana pa nkhaniyi zikonzedwe kudzera m'Maunduna a za Achinyamata, Masewero ndi Chikhalidwe cha Anthu ndi Zoti Pasakhale kusiyana pakati pa Amayi ndi Abambo Pantchito, Ana ndi Zosamalira Anthu ndipo kuti pakhale magulu awiri. Gulu loyamba likhale la ana a zaka za pakati pa 11 ndi 17 ndipo gulu lachiwiri likhale la Achinyamata a zaka za pakati pa 18 and 25. Iwo adapempha kuti magulu awiri onsewa adzakhale nawo pa zokambirana za m'maboma.

Pa zokamirana zonse anthu adasosonyeza kukhumudwa kwawo ndi momwe aphungu a kunyumba ya malamulo akusulutsira Malamulo Oyendetsera Dziko lino chifukwa cha magawo ndi ndime zambirimbiri za malamulowa zomwe nyumba ya malamulo idasinthu kuyambira m'chaka cha 1994. Anthu ena amafunsa kuti phindu lofunsira anthu a kumudzi za malamulowa nkotani chonsecho ngakhale anthuwo atapereka maganizo awo, pamapeto pake aphungu akunyumba ya malamulo adzavomereze kapena kukana kuti malamulowo asinthedi, mokomera iwo.

## 2.2 Msonkhano Woyamba Waukulu Wounika Malamulo Oyendetsera dziko Lino

Zolinga za msonkhanowu ndi zitatu. Choyamba ndi kukhazikitsa kapena kuyambitsa ntchito younika ndi kusintha malamulow chifukwa ndi ntchito yokhudza dziko lonse. Chachiwiri ndi kufuna kuti nthumwi zigwirizane malamulo oyenera kuwasintha. Cholinga chachitatu ndi kugwirizana kuti kodi ntchito yosintha malamuo ipitirira bwanji nanga zikhala bwabji ngati nthumwi zitagwirizana kuti zisinthe malamulo ena omwe ngotetezedwa kuti asasinthidwe.

Anthu onse amene adatenga nawo mabli pa misonkhano yomva maganizo awo pa za kusintha kwa malamulo adavomereza kuti pafunika kuti pakhale msonkhano wa dziko lonse wounikanso malamulo oyendetsera dziko lino. Ena amati msonkhano umenewu ngofunika kwambiri pa ntchito yolimbikitsa umodzi pakati pa anthu am'dziko lino malinga ndi mavuto a za ndale omwe alipo.enanso amati msonkhanwo usonyeza chidwi chomwe Boma lili nacho pa ntchito younikanso ndi malamulo oyendetsera dziko lini chifukwa chakuti akautsegulure ndi mtsogoleri wa dziko.

Anthu ena msonkhanowu ndi wofunika kwambiri uthandiza kuika pamodzi maganizo a atnu ochokera m'ziagwo zones zitatu ndiponso udzathandiza kuti anthu osiyanasiyana atengepo mbali pa nthito yokonzanso malamulo oyendetsera dziko lino

posayang’anira kulemera kapena kusauka, udindo, komwe amachokera ngakhalenso zipembedzo zawo.

Uwu ndi msonkhano womwe anthu adzapereke madandaulo awo okhudza momwe malamulowa tikuwagwiritsira ntchito.

Komabe anthu ambiri amati anthu nthumwi 150 zomwe zidzaitanidwe kuti zidzachite nawo msonkhanowo zachipa kwabiri, komabe amavomerza kuti zokambiranazo osati kuchuluka kwa anthu ndizo zili zofunika kwambiri. Bungwe la Law Commission lidapemphedwa kuti likhazikitse njira zamakono zofalitsira mauthenga pogwiritsa ntchito makina a komputa (website) kuti anthu ambiri am’dziko muno ndi omwe ali kunja kwa dziko lino adzathe kutenga nawo mabli pa zokambiranazo.

Bungweli adalipemphanso kuti likonzekera msonkhanowu mokwanira kuti nthumwi zizikakamba maganizo a anthu omwe akuwaimirira osati maganizo awo. Bungweli lidauzidwanso kuti kuti kumsiknhanoku kusakachuluke anthu oimira zipani za ndale. Choncho nthumwi zidapereka maganizo oti zipani zokhazo zomwe zili mkaundula wa zipani ndiponso zikugwira ntchito ndi zomwe adzaziitane ke msonkhanowu. Bungweli lidalangizidwanso kuti lidzaitanenso ophunzira a ku Yunivesite ku msoknhanoko.

## 2.3 Ntchito Yosintha Malamulo ndi Msonkhano Wachiwiri Wounika Malamulo a dziko lino

Ntchito yosintha malamuo idzatsata ndondomeko yomwe bungwe la Malawi Law Commission lidakhazikitsa. Idzayamba ndi kusankha akatwiri oti adzagwire ntchitoyi mwaganyu ndipo azidzakomana kamodzi pa mwezi kukambirana nkhani zokhudza malamulo nthumwi kumsonkhano zidati asinthe. Pamapeto pake zidzalemba lipoti loyamba lomwe lidzaperekedwe ku msonkhano wachiwiri wa dziko lonse kuti nthumwi ziliunike ndi kupereka maganizo awo otsiriza, lipotilo asanalitumize ku bungwe ya Nduna za Boma komanso ku Nyumba ya malamulo.

Bungwe Lapaderali lidzachititsanso misonkhano m’maboma kuti likamve maganizo a anthu pa zomwe nthumwi zidagwirizana ku msonkhano wayamba wa dziko lonse.

Anthu adatsindika kufunika kosankha anthu odziwa bwino ntchito yawo kuti akhale m’bun gwe la padera lounikanso malamulo adziko lino.

## CHIGAWO CHACHIWIRI

## MUTU WOYAMBA

### 1. DZIKO LA MALAWI

#### 1.1 Chiyankhulo cha mtundu wa Amalawi

Malamulo Oyendetsera dziko la Malawi safotokoza za Chiyankhulo cha dziko la Malawi. Pazokambiranna anthu adafotokoza kuti chiyankhulo cha Chichewa chimatengedwa ngati chiyankhulo cha Amalawi ngakhale malamulo sakunena choncho. Choncho anthu adafotokoza kuti ndime yachiwiri ya Malamulo Oyendetsera Dziko Lino iyenera kuvomereza Chichewa ngati chiyankhulo cha Amalawi. Iwo amati izi zitha kumodzi pakati pa anthu onse m'Malawi muno.

#### 1.2 Kusiyanitsa pakati pa nthambi za Boma

Ndime 7, 8 ndi 9 za malamulo Oyendetsera dziko lino zimafotokoza kuti payenera kukhala kusana pa ntchito ndi mphamvu pakati pa Nthambi Yolamula, nthambi Yopanga Malamulo ndi Nthambi Yoweruza. Izi ndi nthambi zitatu za boma la Demokalase monga boma la Malawi. Nthambi Yolamula ili ndi udindo yoyambitsa ndi kukwaniritsa ndondomeko ndi malamulo opindulira anthu zomwenso zikugwirizana ndi malamulo Oyendetsera dziko lino. Udindo woyamba wa nthambi Yopanga malamulo ndi kuvomereza kukhala malamulo omwe nthambi Yolamula inaganiza. Ndipo udindo woyamba wa Nthambi Yoweruza ndi kutanthauzira, kueteza ndi kuonetsetsa kuti anthu akutsata Malamulo Oyendetsera Dziko komanso malamulo ena onse. Motero nthambi zitatuzi zimaonana momwe iliyonse ikugwirira ntchito.

Pazokambirana zosiyanasiyana anthu adapempha bungwe la law commission kuti liunikenso bwino malamulo okhudza kusiyanitsa kwa kagwiridwe ka ntchito pakati pa nthambi zitatuzi kuti pasakhale kulowererana. Anthuwa amapereka chitsanzo kuti nthawi zina aphungu wamba amalowerera udindo wa

nthambi yolamula pomayambitsa mfundo zoti nYumba ya malamulo izxivomereze kuti akhale malamulo. Iwo adati malamuo Oyendetsera Dziko lino aspereke mwayi kwa aphungu wotulutsa maganizo awo m'nyumba ya malamulo kuti nyumba iwavomereze kuti akhale malamulo, chifukwa ndi udindo wa Nthambi yokhayo yolamula kuchita zimenezo.

## 1.3 Mfundo Zofunikira

Ndime 13 ya malamulo oyendetsera dziko lino amafotokoza mfundo zosiyanasiyana zokhudza maufulu a anthu kuyambira Mfundo yoti pasakhale kusiyana pakati pa amayi ndi abambo pa ntchito mpaka zoti mfundo yokhudza ulamuliro wabwino. Pazokambirana zosiyanasiyana anthu adafotokoza kuti nkofunika kuonjezerapo mfundo yoti dziko lino lizikhala lodzidalira pa chakudya nthawi zones ngati mfundou imodzi yofunika kwabwiri ndipo kuti ikhale poyambirira penipeni chifukwa dziko la Malawi mfundo ya chakudya ndi yofunikira kwambiri kuposa china chilichonse.

## CHIGAWO CHACHIWRI

## 2. UFULU WA CHIBADWIDWE WA ANTHU

### 2.1 Chilango Chonyonga

Ndime 16 ya malamulo Oyendetsera dziko lino imafotokoza kuti “munthu aliyense ali ndi ufulu wokhala ndi moyo ndipo palibe munthu wina aliyense amene ayanera kumuchotsera moyo wakeyo”. Koma lamulo lomwelo limalola kuti munthu atha kunyongedwa ngati khoti litalamula chifukwa choti wapezeka wolakwa pa mlandu woopsa kwambiri.

Komabe ndime 44 (1) (a) ya malamulo omwewa imati “ufulu wokhala ndi moyo” suyenera kulandidwa kwa munthu mwa njira iliyonse. Choncho pali kutsutsana pakati pa Ndime 16 ndi ndime 44, zomwe nzofunika kuzionanso bwino.

Pokambirana za chilango chonyonga, anthu odziwa za mamalulo adati ndibwino kuti chilangochi choumiriza koma kuti kukula kapena kuopsa kwa mlandu womwe munthu adapalamura ndiko kuzichititsa kuti alndire chilango chonyongedwa kapena ayi. Mafumu a m’Chigawo Chapakati adati chilangochi n’chongofunika kuchichotsa chifukwa nchankhanza ndipo sichindulira aliyense. Iwo adati mafumu akuyesetsa kuti chilango chamtunduwu chithe m’Chigawochi. Mabungwe ogwira ntchito zolimbikitsa za ufulu wachibadwidwe wa anthu akugqirizananso ndi mafumuwa.

### 2.2 Maukwati opanda Nkhoswe

Ndime 22 ya Malamaulo Oyendetsera dziko lino imavomereza ndi kuteteza banja ngati komwe mtundu wa dziko umayambira. Pachifukwachi, malamulowa amavomereza maukwati a mitundu itatu: ukkwati wa mchatho, ukwati womangidwa kumudzi motstat myambo ya mitundu ya anthu ndi maukwati opanda nkhoswe.

Mabanja opanda nkhoswe amavomerzeka kapena kulongosoka akamatha, makamaka chifukwa cha imfa ya m’modzi mwa awiriwo kapena ngati watha mwa njira zina, ndipo izi zimachitika motsatatnsokutalika kwa nthawi yomwa awiriwa akhalira limodzi. Mafumu adanenetsa kuti mabanja a mtunduwu amalimbikitsa mchitidwe wa chiwerewere pakati pa anthu. Iwo adati maukwati opanda nkhoswe amatsutsana ndi chikhalidwe ndi mayiambo ya Chimalawi yomwe nagti chinthu cholemekezeka chomwenso chimabweretsa chibale pakati pa mabja awiri.

Kumbali yawo, achinayamata ndi ana adati malamulo oyendetsera dziko asmavomereze maukwati opanda nkhoswe

chifukwa amalimbikitsa ana kuti azichita zinthu zosayeneras kuphatikizapo mchitidwe wa chiwerewere.

Koma akulualuklu odiwa za malamulo adali ndi maganizo awoawo pankhaniyi. Iwo akuti maukwati oterewa amateteza mayi kwa amuna omwe amanamizira ndi okwatira pomwe m'maganizo mwawo sizili choncho. Choncho kwa iwo mabanja a mtunduwu ngabwino ndipo sasukulutsa ulemu wa banja, ngati atatengedwa ngati njira yoteterzera akazi ku amuna achinyengo.

## 2.3 Ufulu Wochita ndale

Ndime 40 (2) ya malamulo oyendetsera dziko lino imafotokoza kuti Boma liyenera kupereka ndalama ku chipani chilichonse cha ndale chomwe chili ndi mpando umodzi mwa mipando khumi iliyonse mnyumba ya malamulo kuti chipanicho chizigwirira ntchito zake. Koma ngakhale zili choncho, Lamulo Lokhudza Zipani za ndale silikambapo chilichonse zokhudza ndalama zomwe Boma liyenera kuperka ku zipanizi.

Anthu pa misonkhano adati payenera kukhala ndondomeko zabwino zofotokoza kuchuluka kwa ndalama komanso momwe Boma liyenera kuperekera ndalamazo ku zipanizi. Mwachitsanzo, akuluakulu adziwa za malamulo adati ndalama zomwe zipani zizilandira zizigwirizana ndi mipando yomwe zili nayo mnyumba ya malamulo. Maganizo ena adali oti ndibwino kuti ndalama zizipita ku dera lomwe phungu amaimira mnyumba ya malamulo osati ku chipani.

Akuluakulu a za malamulu adatsutsa mfundo yoti chipani chilichonse cha ndale chomwe chili mkaundula wa zipani chizilandira ndalama kaya chili ndi aphungu kunyumba ya malamulo kapena ayi. Iwo adati izi zitha kuchititsa kuti anthu ena a maganizo opotoka azingolembetsa zipani ncholinga choti azingolandira ndalama zaulele kuchokera ku Boma chonsecho chipani chawocho sichikugwira ntchito ndipo anthu sakuchidziwa. Panalinso maganizo oti ndalama za Boma nthawi zonse zimakhala zochepa choncho nkufunika kukhazikitsa ndondomeko zokhudza momwe Boma liziperekera ndalama ku zipani za ndale. Ena adati kuti malamulo okhudza ndalama zomwe zipani ziyenera kulandira kuchokera ku Boma azitha kusintha mkati mwa zaka zisanu mogwirizana ndi kuchuluka kwa aphungu omwe zipanizo zili nawo mnyumba ya malamulo pa nthawiyo. Iwo adati akuganiza motero pozindikira kuti chiwerengero cha aphungu oimira chipani chakutichakuti mnyumba ya malamulo chimatha kusintha malinga nkuti nkuti aphungu ena amatha kutuluka mchipani chawo nkulowa chipani china ,komanso chifukwa cha imfa za aphungu ndi zisankho zapadera.

Mfundo yotsiriza pa nkhaniyi idali yoti payenera kuti pakhale ndondomeko zothandiza kuona kuti zipani zikugwiritsa nchito ndalama zochoka ku Boma moyenera. Choncho anthu adanena kuti payenera kukhala lamulo ndime m'Malamulo Oyendetsera Dziko lino kapena mu Lamulo Lokhudza Zipani Zandale zikugwiritsa ntchito ndalamazo mwachilungamo ndipo kuti Mkulu Wounika momwe Mabungwe, Madipatimenti ndi Mabungwe a Boma agwiritsira ntchito ndalama , azithanso kuunika momwe zipani za ndale zizigwiritsira ntchito ndalama zochokera ku Boma.

## 2.4. Ufulu wokhala Nzika ya Dziko la Malawi

Ndime 47 ya malamulo Oyendetsera dziko lino imafotokoza kuti munthu atha kukhala nzika ya dziko la Malawi chifukwa choti wabadwira kuno, polemebtsa dzina lake mkaundula wa anthu omwe si Amalawi koma mdi nzika za dziko lino, chifukwa choti makolo ake ndi kapena adali Amalawi, chifukwa cha ukwati komanso chifukwa cha chilengedwe. Mavuto ambiri amabwera pamene munthu wakhala nzika ya dziko lino kudzera mu ukwati, chifukwa chakuti lamulo Lokhuzda Unzika wa munthu silivomereza kwenikweni kuti munthu akhale nzika wa dziko lino mwa njirayi. Chachiwiri nchakuti ndi akazi okha omwe akwatiwa ndi amuna omwe ndi Amalawi ndipo akawniritsa ndondomeko zonse zomwe zili m'ndime 13 (1) ya lamuloli omwe amaloledwa kukhal nzika za dziko lino. Zina mwa ndondomekozi ndi zoti mkaziyo khale kuti wakhala mdziko muno kwa zaka zisanu zotsogozana, azitha kumva ndi kuyankhula chimodzi mwa ziyankhulo za kuno ku Malawi kapena Chingerezi ndiponso wa khalidwe la bwino komanso wa makhalidwe ovomerezeka ngati mkazi.

Pali kutsutsana kwakukulu pakati pa malamulo Oyendetsera dziko lino ndi Lamulo Lukhudza Anthu ofuna kukhala nzika za dziko lino. Mfundo yoyamba ndi yakuti ukwati pawokwa ndi chinkhu chokwanira chomuyenereza munthu kukhala nzika ya dziko lino potsata malamulo Oyendetsera Dziko Lino pomwe mu Lamulo Lokhudza Anthu ofuna Kukhala Nzika a dziko lino, ukwati ndi chinthu chimodzi choyenera kuchiganizira kuti dzina lake lilowe mkaundula waanthu omwe si Amalawi koma ndi nzika za dziko la Malawi. Chachiwiri nhakuti ndi akazi okha omwe akwatiwa ndi amuna omwe ndi Amalawi osati amuna omwe akwatira akazi omwe ndi Amalawi omwe amaloledwa kukhala nzika za dziko lino, chonsecho malamulo oyendetsera dziko lino sasiyanitsa pakati pa nzika za chikazi kapena zachimuna.

M'chaka cha 1996 bungwe la aphungu achikazi lidapereka maganizo awo ku bungwe la Law Commission oti Lamulo Lokhudza Anthu Omwe Akufuna kukhala nzika za dziko lino

lisinthidwe kuti ndime zomwe zikundereza kapena kusankha amayi zichoke. Iwo mapadera adati Ndime 16 ya Lamuloli alisinthe kuti amuna a omwe si amalawi koma akwatira akazi Achimalawi ndipomnso komanso akazi omwe si Amalawi koma akwatiwa ndi amuna a Chimalawi azipatsidwa mwayi wofanana pofuna kuwavomereza kuti akhale nzika za dziko lino. Magaizowa adaperekedwa pozindikira kuti malamulo Oyendetsera dziko lino salola kuti munthu wina aliyense azisankhidwa mwa mtundu wina uliwonse ndiponso pozindikira kuti Ndime 20 ya Malamulowa imati munthu wina alyense kaya ndi wamkazi kaya ndi wamwamuna ayenera kuonedwa mofanana ndipo sayenera kusankhidwa mwa njira iliyonse chifukwa ndi wamkazi kapena wamwamuna. Koma komiti ya nduna za Boma, pa zifukwa zodziwa yokha, idakana kuti lamuloli lisitnhidwe pofuna kuletsa amuna ena omwe ndi akamberembere omwe akadamanamizira kukwatira akazi a chimalawi ncholinga chongofuna kupeza mwayi wokhla nzika ya dziko la Malawi. Pa chifukwa ichi pali maganizo oti ndibwino kuti akazi omwe si Amamalwi koma akwatiwa ndi amuna a Chimalawi asmaloedwe kukhala nzika za dziko lino koma ktui azingopatsidwa mwayi wokhala nawo m'dziko muno, chimodzimodzi ngati amuna omwe si Amalawi koma adakwatira akazi a Chimalawi.

Nduna za Boma Komanso akuluakulu odziwa za malamulo adagwirizana ndi maganizo amenewa ndipo adatsindika kufunika kuonetsetsa kuti anthu obwerawa asaloledwe kukhala nzika za dziko li no chifukwa choti akwatira kapena akwatiwa ndi M'malawi koma kuti azipatsidwa chilolezo chokhala nawo mdziko muno.

## 2.5 Ufulu woti Amayi azikhala aphungu a kunyumba ya malamulo

Iyi inali imodzi yomwe idakhudza anthu ambiri pa zokambirana zosiyanasiyana. Pakali pano, mnyumba ya malamulo muli aphungu 193 ndipo mwa amenewa aphungu aakazi alipo 27 okha. Izi zikutanthauza kuti mwa aphungu zana limozdi aliwonse, aphungu aakazi alipo khumi ndi awiri basi, chomwe chili chiwerengero chochepa kwambiri poyerekeza ndi zomwe maiko a m'bungwe la SADC adagwirizana komanso zomwe Migwirizano ina yokhudza maiko osiyansiyana a padziko lapasi yomwe Boma la Malawi lidasainira zoti mwa aphungu zana limodzi lililonse, makumi atatu azikhala amayi. Izinso sizikugwirizana ndi chiwerengero cha anthua dziko, chomwe chiwerengero cha amayi chiamposa cha abambo.

Mabungwe ogwira ntchito zolimbilikitsa za ufulu wa chibadwidwe wa anthu adapereka maganizo othandiza kuthetsa vutoli. Iwo adati Boma la Malawi liganizire zoti zipani zizikhala ndi

chiwerengero chiwerengero cha mipando yomwe zizikhala nayo mnyumba ya malamulo ndipo potero chipani chilichonse chisankha chokha chiwerengero cha aphungu aakazi omwe chikufuna kukhala. Mabungwewa adati mwanjirayi, nkwapafupi kuti dziko la Malawi likwaniritse zoti mwa aphungu a kunyumba ya malamulo zana limozdi alionse, makumi atatu akhale aakazi.

Bungwe la aphungu achikazi lidavomerezanso njira imeneyi pozindikira kuti ndi m'mene zisankho za aphungu a kunyumba ya malamulo zimayendera m'dziko muno, nkovuta kukwaniritsa zimenezi. Iwo adapereka zifukwa zingapo. Mwchitsanzo, iwo adafotokoza kuti si amayi ambiri amene amafuna kudzionetsera kapena kubwera poyera kuti anthu awaganizire powasankha pa mipando, mwina chifukwa cha mantha, kudzikayikira komanso momwe ndale za kuno lu Malawi zimayendera sizilola kwenikweni kuti munthu wamkazi atenge mnawo mbali.

Bungwe la aphungu achikazili lidaperekansomaganizo ena oti mwina ndibwino kuti kunyumba ya malamulo kukhale mipando ingapo yomwe amyi okhaokha azilimbirana. Njira ina nkukhala ndi Madera ena omwe aphungu ake azikhala amayi okhaokha basi. Iwo adapereka zitsanzo za maiko omwe zoterezi zikuchitika ndipo zikuyenda bwino monga Uganda, Tanzania ndi Rwanda.

## 2.6 Kugonana pakati pa akazi ndi amuna

Ndime 20 ya malamulo Oyendetsera dziko lino amaletsa zoti anthu azisankhana chifukwa cha mtundu, khungu, chifukwa choti wina ndi wamwamuna kapena wamkazi, chiyankhulo, kapena chifukwa cha maganizo ake pandale kapena pa zinthu zina zilizonse. Potsata ndime imeneyi, anthu ena adapereka maganizo oti malamulo a dziko lino ayanera kusintha mogwirizana ndi malamulo Oyendetsera dziko kuti pasakhale kusankhana chifukwa choti akufuna kumagonana ndi mkazi kapena mwamuna nzake. Ndime 153 ya malamulo a dziko lino amaletsa mchitidwe wogonana wotsutsana ndi chilengedwe. Izi zimakhudza kugonana ndi mwamuna kapena mkazi koma osati momwe Mulungu adalengera kuti zizikhalira. Munthu akapezeka ndi mlandu wa mtunduwu amamangidwa zaka khumi ndi zinayi ndi kukagwira ntchito ya kalavula gaga kundende.

Ndime 156 ya malamulo a dziko lino imaletsanso kuti amuna azigonana okhaokha. Chocho munthu wamwamuna saloledwa kugonana kapena kuchita zinthu zosonyeza chikondi ndi mwamuna mnzake pagulu kapena pamalo obisika. Munthu akapezeka akuchita zoterezi amamangidwa ndi kukangwira ntchito ya kalavula gaga kundende kwa zaka zisanu.

Pa zokambirana ndi mabungwe olimbikitsa za ufulu wa chibadwidwe wa anthu, mabungwewa adakana zoti malamulo azivomereza zoti amauna kapena kazi azigonana papena kukwatirana okhaokha. Bungwe la aphungu aakazi, oimira chipani cha DPP komanso anthu a m;mudzi mwa Gumulira mdera la Mfumu Mlonyeni ku Mchinji adakanaso zimenezi kuhatikizapo zoti anthu amane amakhulupirira zinthu za mtunduwu akhale ndi ufulu wochita zimenezi. Mafumu mzigawo zonse zitatu adakananso zimenezi. Iwo adti zoterezi zitha kunyozetsa ndi kusukulutsa ulemu wa banja. Choncho mafumuwa adachenjeza bungwe la Law Commission adalichenjeza kuti liusatengere kapena kukopera makhalidwe onyansa a kunja omwe ndi otsutsana ndi miyambo ndi chikhalidwe komanso zipembedzo za anthu a mdziko lino.

## 2.7 Kugwira munthu womuganizira kuti waphwanya lamulo ndi kumuzenga milandu mwachilungamo

Ndime 42 ya malamulo oyendetsera dziko lino imafotokoza ndondomeko zogwirira munthu yemwe akuganiziridwa kuti walakwa, kumanga komanso kuti ayimbidwe mlandu mwachilungamo ndi kuti munthu aliyense amene wagwidwa ayenera kuti apite kukhoti kuti akamutsegulire mlandu kapenda akauzidwe chifukwa chomwe wagwidira pasanathe masiku awiri chimugwirire. Ngati masiku awiri akwana tsiku la tchuthi kapena kumapeto a sabata, munthuyo ayenera kupita kukhothiko tsiku lotsatira la ntchito kapena tsiku lolemba.

Nkhani imeneyi ikuvuta makama masiku ano pamene boma la Malawi ndi la zipani zambiri. A mbali ya boma amati masiku awiri achepa kwambiri kuti pakhale zofufuza zokwanira ndi iwo amaganiza kuti koma atakhala masiku asanu ndi awiri (7). Maganizo a anthu ambiri akuti apolisi sadatsatire mokwanira lamuloli.

Koma ena amati masiku awiri ndi okwanira kuti apolisi amuuze munthu chomwe walakwa ndi kupita naye ku khoti. Anthu ena adapereka maganizo oti apolisi adzigwira munthu amene akumuganizira kuti walakwa pamene ali okonzeka kupita naye kukhoti. Iwo akuti izi zingathandize kuti ufulu wa munthu usaphwanyike.

Pa zokambiranazo, nkhaniyi inatuluka pa misonkhano iwiri yokha; wa akuluakulu ndi wa anthu a m’mudzi mwa Gumulira mdera la mfumu Mlonyeni ku Mchinji. Pa msonkhano wa akuluakulu a za malamulo, iwo anati masiku awiriwo asasinthe chifukwa ndi njira imodzi yotetezera ufulu wachibadwidwe wa munthu wogwidwayo. Choncho iwo adati sibwino nthawi yosungira munthu asanapite naye kukhoti asamyiwonjezere popanda chifukwa chenicheni – pokhapokha ngati milandu yake

ili yowopseza chitetezo cha munthu. Iwo adatinso malamulo oyimbira munthu mlandu ayenera kusintha kuti apolisi azimuuzulatu munthu chomwe akumuganizira kuti walakwa panthawi yomugwira ndikumuuzanso za ufulu wake ngati munthu woti akumuganizira kuti waphwanya malamulo a dziko.

Koma anthu a kwa Gumulira adagwirizana ndi maganizo a Boma ndipo adati ndi bwino kuti munthu pazipita masiku khumi asanapita naye ku khoti kuti apolisi akhale ndi nthawi yokwanira yofufuza za mlanduwo. Iwo adati izi zingathandize kuti apolisi asamangopereka belo mwachisawawa komanso kuti mbanda ndi mbava zisamasowetse anthu mtendere podziwa kuti zikagwida zikatuluka mwachangu pa belo.

## 2.8 Ufulu wa Maphunziro

Ndime 25 ya malamulo oyendetsera dziko lino imati munthu aliyense ali ndi ufulu wouphunzira ndipo kuti maphunziro a msukulu za pulayimale asachepere zaka zisanu. Ndime 13 ya malamulowa imati boma liyenera kupereka zinthu zonse zofunikira komanso zokwanira ku ntchito za maphunziro ndi kuti boma likonze ndondomeko zothandiza kuti maphunziro a ku pulayiomale akhale oumiriza ndi aulere kwa m'Malawi aliyense.

Anthu ambiri adapereka madandaulo pa nkhaniyi. Pamsonkhano wa ana ndi achinyamata ku Lilongwe, iwo adapempha boma kuti lionetsetse kuti maphunziro mdziko muno akhale oumiriza kuti mwana aliyense akhale ndi mwayi wophunzira. Koma akuluakulu a za malamulo adati akuona kuti ndilokonzeka kukhazikitsa lamulo loti maphunziro akhale oumiriza muno chifukwa palibe ndondomeko zothandiza kuonetsetsa kuti lamuloli luktsatidwa.

Pankhani ya maphunziro aulere, ana ndi achinyamata adati sakukhutira ndi momwe maphunzirowa akuyendera. Iwo adato zoona zake nzakuti maphunzirowa siaulere chifukwa ophunzira amaumirizidwa kupereka ndalama zochitira zinthu zosiyanasiyana kususkulu, zomwe zimalepheretsa ana ambiri makamaka a m'madera a m'midzi kuti aphunzire. Iwo adapempha boma kuti liunikenso nkhaniyi kuti maphunzirowo akhaledi aulere.

Ana ndi achinyamata adatinso ndi bwino kuti maphunziro a ku pulaimale atakhala zaka zosachepera zisanu ndi ziwiri osati zisanu chabe. Pa msonkhano womwewo, nkhani ina yomwe idatuluka idali yokhudza maphunziro omwe ophunzira amaphunzira msukulu za pulaimale ndi sekondale. Iwo adapempha boma kuti liunikenso maphunzirowa ndi kuwasintha kut agwirizane ndi momwe zilili panopa poopa kusinthasintha zomwe zimangosokoneza ophunzira. Iwo adatinso boma

liyenera kusintha nthawi yamaphunziro. Akuluakulu a za malamulo adati boma liyenera kuika ndondomeko zothandiza kuti ana olumala, akhungu ndi ena ovutika mnjira zina azitha kuphunzira mosavuta.

## 2.9 Ufulu wa Achinyamata

Malamulo oyendetsera dziko lino amati ana, amayi ndi an alumala ndi anthu oyenera chitetezo chapadera. Pamsonkhano wa achinyamata ndi ana, iwo adati malamulowa sakupereka chitetezo chapadera kwa achinyamata. Choncho iwo adati ana ayenera kukhalanso mugulu la athu ofunika chitetezo chapadera m'malamulo oyendetsera dziko lino.

## 2.10 Msinkhu Woyenera Kuti Munthu Alowe M'banja

Ndime 22 (6), 7 ndi 8 za malamulo oyendetsera dziko lini zimafotokoza za msinkhu woyenera kuti munthu alowe m'banja. Gawo 6 la ndime 22 limati munthu aliyense yemwe ali ndi zaka zakubadwa zopitirira khumi ndi zisanu ndi zitatu (18) asakanizidwe kukwatira kapena kukwatiwa ngati atafuna kutero. Ndipo Gawo 7 la ndime yomweyi munthu amene ali ndi zaka za pakati pa 15 ndi 18 zakubadwa apemphe chilolezo cha makolo ake ngati atafuna kulowa m'banja. Koma Gawo 8 la ndime 22 imakaniza ukwati ngati m'modzi mwa ofuna kukwatiranawo sadakwanitse zaka 15.

Achinyamata ndi an adafotokoza kuti lamuloli limalimbikitsa kuti ana ang'onoang'ono azilowa m'banja nagti azipempha chiloloezo cha makolo. Iwo adati izi zikulimbikitsa mchitidwe woipa pakati pa makolo woumiriza ana awo makamakaaakazi kuti akwatiwe ngati njira yopezera ndalama. Iwo adati uku ndi kuphwanya uful wa maphunziro wa ana ndipo adati malamulo asalole ana amene sadakwanitse zaka 18 kulowa m'banja. Kuonjezera apo iwo adati achinyamata a zaka za pakati pa 18 ndi 21 azipempha chilolezo cha makolo awo akafuna kulowa m'banja pomwe achinyamata opitirira zaka 21 akhale ndi ufulu wokwatira kapena kukwatiwa popanda wina womuletsa.

## 2.11 Ufulu wa Ana

Ndime 23 imati ana ndi anthu omwe sadakwanitse zaka 16 zakubadwa. Choncho lamulo limapereka ufulu wapadera kwa anawa ndipo limateteza ana ku mchitidwe wopondereza ana powagwiritsa ntchito zosagwirizans ndi msinkhu wawo nkumawalipira malipiro ochepa, kaya mchitidwe wina uliwonse wa nkhanza, ntchito kapena chilango chosagwirizana ndi msinkhu wawo.

Achinyamata ndi ana adati msinkhu womwe munthu ayenera kutengedwa ana uyenera kusintha kuchoka pa zaka 16 kufika pa zaka 18. Achipani cha DPP ndi akuluakulu ena a boma adagwirizana ndi maganizowa ndipo adati izi ziyenera kugwirizana ndi zomwe Mgwirizano wa Maiko amu Africa pa za ufulu wa ana umanena pa za msinkhu wa munthu amene ayenera kutengedwa ngati an. Iwo adatinso payenera kukhala kalembera woumiriza wa an akangobadwa.

## 2.12 Ufulu wosasankhana

Ndime 20 ya malamulo oyendetsera dziko lino imaletsa kusankhana pakati pa anthu pa chifukwa cha mtundu wina uliwonse ndipo umapatsa mphamvu boma zokhazikitsa malamulo oonetsetsa kuti lamuloli likutsatidwa. Izi zikutanthauza kuti munthu wina aliyense sayenera kusankha mzake ngakhale zitavuta zitatani. Koma pa mlandu wa pakati pa mkulu wolangiza boma pa nkhani za malamulo ndi chipani cha MCP, bwalo lalikulu la milandu la Supulimu ludagamula kuti “Ndime 20 ikutanthauza kuti anthu sayenera kusankhana ngati palibe chokwanira ndi chomveka bwino shomusankhira munthu”. Komit ya bungwe la United Nations yoona za ufulu wa anthu pandale la ICCPR idagwirizana ndi khoti lalikulu ndipo idaonjeza kuti “ufulu woti munthu aliyense ayenera kutetezedwa popanda kusankhidwa sutanthauza kuti kuti munthu sangasankhidwe ngati patafunika kutero. Choncho kumusankha munthu ngati pali zifukwa zokwanira zikuphwanya lamuloli”.
Anthu adafotokoza kuti potsata zomwe bwalo la mulandu la Supulimu lidagamula ndi bwino kuti ndime 20 izifotokoza kuti munthu asasalidwe mophwanya malamulo kapena mopanda chilungamo, mogwirizana ndi momwe malamulo oyendetsera maiko ena monga South Africa, Zimbabwe ndi Zambia amanenera.

Panalinso mfundo ziwiri zomwe zidatuluka pankhani. Anthu adanena kuti malamulo asinthe kuti aziti munthu asasankhidwe potengera dziko la kwawo osati “dziko lomwe amachokera” monga momwe zinthu ziliri panopa.

Nkhani ina yomwe idatuluka inali yokhudza matenda a EDZI ndi kachirombo koyambitsa matendawa. Iwo adati popeza kuti matendawa akhudza dziko lonse, nkofunika kuti m’malamulo oyendetsera dziko lino mukhale ndime yoteteza anthu omwe akudwala kapena akukhudzidwa ndi matendawa kuti asamasalidwe.

## 2.13 Ufulu wa pantchito

Ndime 31 (1) ya malamulo oyendetsera dziko lino imapereka ufulu kwa munthu wolembedwa ntchito mwachilungamo ndi kumagwira ntchito m'malo otetezedwa komanso kuti azilandira malipiro ogwiriza ndi ntchitoyo.

Gawo 3 la ndimeyi ikutsindikiza za ufulu woti munthu aliyense azilandira malipiro ofanana pantchito yofanana posayang'anira kuti wina ndi wamkazi kapena wamwamuna, wolumala kapena ayi kapena mtundu wake.

Anthu adati nkofunika kuti ndime imeneyi ilembedwenso kuti nkhani zofanana zikhale pamodzi kuopa kosokoneza anthu. Mwachitsanzo, adati nkhani zokhudza malipiro zikhale m'gawo limodzi ndipo nkhani zokhudza chitetezo ndi chilungamo patchito zikhalenso m'gawo limodzi.

## 2.14 Kuchita zinthu mwachilungamo

Ndime 43 ya malamulo oyendetsera dziko lino imati munthu ayenera kupatsidwa chilango mwachilungamo komanso motsata ndondomeko. Komanso imafotokoza kuti munthu amene wapatsidwa chilangoyo ayenera kudziwitsidwa zifukwa zake polemba.

## CHIGAWO CHACHITATU

## 3. NTHAMBI YOPANGA MALAMULO

### 3.1 Seneti

Ndime 49 yoyambirira ya malamulo oyendetsera idati nyumba ya malamulo idzakhala ndi nyumba ya aphungu, nyumba yaing'ono (Seneti) ndi Pulezidenti ngati mutu wa boma. Ndime 68 idati padzayenera kukhala seneti yomwe idzakhale ndi woimira m'modzi m'boma lililonse wosankhidwa mwachinsinsi yemwe adzakhale munthu woti adalembetsa mkaundula wa voti ndipo adaponya nawo voti. Mfumu imodzi ya boma yomwe idzasankhidwe machinsinsi ndi mafumu anzake komanso anthu ena makumi atatu ndi mphambu ziwiri (32) oyimira magulu osiyanasiyana a anthu ndi mabungwe omwe siaboma omwe adzasankhidwe ndi mamembala 66 mwa mamembala 100 aliwonse a nyumbayi, mothandizana ndi komiti yapadera yothandiza posankha anthu oyenera kukhala mamembala a seneti. Seneti imayenera kukhala ndi mamembala makumi asanu ndi atatu (80).

Koma lamulo lokhazikitsa nyumba ya seneti lidachotsedwa m'malamulo oyendetsera dziko lino mchaka cha 2001 pa zifukwa zoti boma lilibe ndalama zokwanira kuyendetsera nyumbayi. Panthawiyo amene adali mkulu wolangiza boma pankhani za malamulo komanso nduna za chilungamo, wolemekezeka a Peter Fatchi, adauza nyumba ya malamulo kuti "ndalama zomwe zidzafunike zoyendetsera nyumba ya seneti nzambiri zedi koti boma silingakwanitse". Mfundo yothets seneti idadza panthawi imene malipiro a aphungu a kunyumba ya malamulo adakwezedwa komanso mphamvu ya ndalama ya Kwacha idatsika kotero kuti kukadafunika ndalama zokwana K500 miliyoni zoyendetsera nyumba ya malamulo pamodzi ndi seneti. Padalibe phungu ndi m'modzi yemwe amene adatchulapo ndime 45 (8) yomwe imati : "Malamulo ano kapena chigawo chogawo sichiyenera kuthetsedwa pachifukwa china chili chonse kapena kusinthidwa kwa mtundu wina uliwonse pokhapokha ngati kusinthako kukugwirizana ndi ndime zina za malamulo ano".

Pachifukwa ichi nthambi ina ya boma idathetsedwa motsutsana ndi malamulo oyendetsera dziko lino.

Maganizo a anthu pa misonkhano yosiyanasiyana adali oti seneti ibwerere chifukwa idzathandiza kuti aphungu azichita zinthu moyenera mogwirizanan ndi ndime 8 ya malamulo oyendetsera dziko lino. Ndime 8 imanti : "Popanga malamulo azidzaganizira zofuna za aMalawi pa zokambirana zawo ndipo azidzaganiziranso phindu lomwe lingadze chifukwa cha lamulolo

> komanso udindo wawo monga momwe malamulo ano afotokozera".
>
> Mafumu ndi mabungwe oimira anthu pa zinthu zosiyanasiyana adati nzokhumudwitsa kuti aphungu satsatira lamuloli chifukwa palibe wowalonda. Mafumu adati seneti ndiyo ikadathandiza kuti mafumuwo azindikire udindo wawo ngati mafumu womwe anthu ambiri saumvetsa.

Bungwe la Malamulo M' Malawi muno (Malawi Law Society) ndi a ku sukulu ya ukachejede adavomerezana pa fundo yoti kukhazikitsa Nyumba ya Mafumu Kukadathandiza kuti kukhale kutolerana pakati pa zipani ndi mgwirizano pakati pa mtundu wa a Malawi. Kumanso nyumbayi ikadathandiza kuti pasmakhale chinyengo mndondomeko zakayendetsedwe ka chisankho zomwe zidakhazikitsidwa mu chaka cha 1994.

Mabungwe ndi anthu ena okhudzidwa adaganiza kuti kuchotsa lamulo lothandiza kuti Nyumba ya Mafumu kunali kosayenera ndiponso zotsutsana ndi Malamulo oyendetsera Dziko lino chifukwa sadatsate ndi kufufuza chifukwa chimene Lamulolo lidayikidwa Mu Malamulo oyendetsera Dziko lino. Nkhani yoti kayendetsedwe ka nyumbayi kukadakhala kuwononga ndalama kuwona ayi potengera ndi m'mene a mphungu a kunyumba ya Malamulo akuchulukira kuchokera pa a phungu 120 mu 1994 kufika pa 194 mu chaka cha 2006. Kuwonjezera tson kwa a phunguwa kwaononga ndalama zomwe zikadamayendetsa Nyumba ya Mafumu. Anthu ambiri omwe adakambapo pa nkhaniyi adaganiza kuti kuchotsa kwa Nyumba ya Mafumu mu malamulo oyendetsera Dziko lino kunali ndale basi osati chifukwa chakusowa kwa ndalama.

Komabe ma Bungwe ndi anthu okhudzidwa pa nkhaniyi adati ngati Nyumbayi ingakhazikitsidwe pafunika kuunika bwino masakhidwe a anthu omwe akalowe mu Nyumbayi kuti yikakhaledi yoyima pa yokha.

### 3.2 Kuchotsa phungu wa kunyumba ya malamulo pampando.

> Ndime 64 yaa 1994 mu Malamulo oyendetsera Dziko lino munali ndondomeko ya m'mene anthu angachotsere phungu wawo ngati akulephera kuwathandiza m'dera lawo. Lamulolo limati-
>
> (1) Phungu aliyense adzayenera kuchottsedwa ndi anthu a Mdela lake potsatira ndondomeko za mu Gawo ili.
>
> (2) Phungu wa ku Nyumba ya Malamulo adzachotsedwa ndi anthu a m'dera lake ngati chikalata cha ndondomeko cha zolakwa zake cha vomerezedwa ndi Bungwe la chisankho, ndipo wodandaulayo-
>
> (a) akhale woti ali mukawundula wa voti m'dela lomwe phunguyo akuyimirira;

(b) ndipo wa onetsetsa kuti maganizo ochotsa phunguyo ngoyenera ndipo chokera kwa anthu osachepera theka la anthu omwe mu kaundula wa voti m'delalo omwe akufuna kuti asakhe wina phungu wolowa m'malo achisakho cha chobwereza.

(3) Ngati kwatheka kuti phungu angachotsedwe Sipika wa nyumba ya Malamulo bungwe la chisankho kuti lilengeze zoti ku deralo khale chisankho chobwereza.

Nyumba ya Malamulo yidachotsa ndimeyi m'malamulo oyendetsera Dziko lino potsata ndime 6 la Malamulo a dziko lino la 1995. Nyumbayi idati Lamuloli lidzangobweretsa chiosokononezo chifukwa anthu ena dzaligwiritsa ntchito molakwika chifukwa cha sanje chabe.

Mabungwe ndi anthu omwe anali nawo pa misonkhano yowunikanso Malamulo oyendetsera Dziko lino adati mkofunika kuti lamulo lochotsa phungu wa ku nyumba ya Malamulo ngati anthu adera lake akuwona kuti sakuwathandiza libwelerenso chifukwa ndilothandiza kuti phungu azigwira nchito yake mokomera dera lake. Iwo adati lamuloli lidayikidwa ndi a Malawi ngati dziko ndipo sikunali koyenera kuti a phungu omwe ndi otumikira anthu komanso anthu ochepa alichotse lamuloli. Mchitidwewu unali osayenera ndipo onse anagwirizana kuti lamuloli libwererenso mu Malamulo oyendetsera dziko lino.

Pa msokhano wa ana achichepere ndi achinyamata a chisodzera omwe udachitira ku Lilongwe omwe udagwirizana ndi kubwezera kwa Lamuloli, adagwirizana kuti ngati Lamuloli litabwerera nkofunika pakhale chitetezo chokwanira kuti anagdzalichotsenso monga adachitira mu chaka cha 1995. Mabungwe owona za ufulu wa anthu adati nkofunika kunenena motsindika kuti lamuloli ndilofuna kuona kuti ufulu wa anthu sukuophwanyidwa ndipo ndi ufulu wawo kuti muthu wowayimirira kunyumba ya Malamulo akuyendetsa zithu mosabisa kathu. Ena amti ngati Pulezidenti kapena Jaji angachotsedwe ngati angalakwire malamulo ena cholepheretsa nchiani kuti aphungu nawo achotsedwe. Enanso anati ngati munthu ali ndi mphamvu zosankha munthu kungalephere bwanji kuti akhale ndi phamvu yotha kuchotsa wa ntchito wake ngati sakugwira bwino ntchito yake. Ndipo ena adati lamulolinso lidzathandiza kuti a phunga athe kukhala ndi khaldwe labwino lotha kulemekeza athu a m'dera mwawo chifukwa anthu mpaka pano sadziwa kuti woyenera kulandira ulemu ndani.

Anthu ena ndi ma Bungwe omwe ankachita nawo misokhano ya kuwunikanso malamulo oyendetsera dziko lino adati kubwerera kwa lamuloli kudzathandiza kuti azikhala pafupi ndi dera lawo asati kuwoneka pa nthawi ya chisankho yokha ayi monga amachitira a phungu ambiri. Konso lamuloli lidzapangitsa kuti a phunguwa azitangwanika ntchito zothandiza dera lawo osati kutanganidwa ndi nkhani za chipani (ndale).

Koma a Bungwe la za Malamulo (Law Commission) ndi Bungwe la a phungu a Kunyumba ya Malamulo a chimai adati ngati lamuloli lingabwezeredwe nkofunika kuonetsetsa kuti payikidwa ndondomeko zokwanira kuteteza a phungu ku anthu ofuna kugwiritsa ntchito lamuloli molakwika ndi cholinga chokwaniritsa zolinga zawo. Motero adati nkofunika kuneneratu ntchito zomwe phungu ayenera kugwira ndiponso kulemba bwino zithu zomwe zingapangitse kuti phungu achotsedwe. Mafumu a kumwera adati ndondomeko za ntchito za phungu ndi zithu zomwe zingapangitse kuti achotsedwe pauphungu ziyenera kulembedwa mu Malamulo oyendetsera kuopa kuti anthu olemphera angamadzatengerepo mwai. Monga kulephera kumakhala kudera komwe akuyimira chingakhale chimodzi mwa zitsanzo zoti zingapangitse kuti anthu amuchotsere phunguwo.

Koma a ku Sukulu ya Ukachejede ya Malawi inachenjeza a Bungwe la Malamulo kuti asalembe zithu mu Malamulo oyendetsera dziko lino zithu zomwe zidzayambitse kusina maganizo patsogolo chifukwa zoterozo sizidzakhudaza a phungu okha ai koma anthu a deralo adzakhudzidwa kuphatikiza Dziko la Malawi lonse. Ngakhale kuti maganizowa ngofuna kuthetsa zinyengo ndi ziphuphu pa nthawi ya zisakho, Lamulo lochotsa phungu ngati sakuchita bwino siloti nkuthetsa mabvuto poganizira m'mene uphawi uliri m'dziko muno.

### 3.3 Phungu wochoka m'chipani chake nkukalowa chipani china chomwe chili ndi aphungu m'nyumba ya malamulo

Ndime 65 (1) ya Malamulo woyendetsera dziko amapereka mphamvu kwa Sipika wa Nyumba ya Malamulo angachotse phungu ngati phunguyo wachoka achoka mchipani chake nkulowa chipani china chomwe chili ndi a phungu M'nyumba ya Malamulo. Koma lamuloli linenapo kathu pa a phungu omwe ndi oima pa okha.

Pa nthawi imene akuluakulu odziwa malamulo amaunika za Malamulo oyendetsera dziko a Bungwe lowona za Malamulo (Law Commission) adalandira maganizo woti kusowa kwa fundo zina mu Malamulo oyendetsera dziko pa nkhaniyi kunali kungoufuna kuti a phungu apeze pobisalilapo akamachoka kuchipani china kupita kuchipani china. Komanso a phungu omwe amati ndi oima paokha sanali kunena zowona ai koma kuti amaopa Lamulo la pa Ndime 65 kuti akawadziwika kuti ndi a chipani ichi ndipo alowa china Munyumba ya Malamulo ndiye kuti awachotsa.

Kuti vuto limeneli lithe a Bungwe loyanga'ana za Malamulo adaganizirapo njira zingapo. Choyamba mchakuti lamuloli ligwire ntchito pa phungu yemwe adasakhindwa kupita ku Nyumba ya Malamulo chifukwa cha chipani komwa mwa iye yekha achoka mchipanicho nkulowa chipani china chomwe chili mu Nyumba ya Malamulo kapena ai. Kachiwiri, phungu yemwe wa chokaq chipani chake nkulowa chipani china mu Nyumba ya Malamulo. Kachtatu, pofuna kuteteza a phungu omwe achotsedwa ndi chipani chawo ku

mchitidwe opanda chilungamo, asachotsedwe ai pokhapokha atkapeza kuti pali chifukwa chencheni choti chipanicho chimuchotsere pa udindo wa uphungu.

Cholinga chenichewni cha maganizo oterewa chinalio kufuna kuonetsetsa munthu anene kuti ndiwomililala payekha pokhaopokha ngati anasakhidwa opanda chipani potsata Malamulo oyendetsera Chisakho cha a phungu ndi Pulezidenti. Choncho phungu aliyense amene wasakhidwa pansi pa chipani payiye yekha mkuchoka chipani ayenera kukafunsanso maganizo a anthu a kudera lakero pochitanso chiosankho chapadera.

Pofuna kuwonetsetsa kuti maganizo a Bungwe owona za Malamulo akutsatidwa, a Nyumba ya Malamulo adasithako zina zokhudza Ndime 65 potsata Lamulo No 8 la 2001 ndipo adawonjezera kuletsa a phungu a chipani chilichonse (osati chipani chokha chomwe chiri mu Nyumba ya Malamulo chokha) komanso bungwe lomwe zolinga zawo ndi za ndale. Nyumbayi idatero pa zifukwa zingapo. Choyamba chinali kuteteza phamvu za chipani munyummba ya Malamulo potero anthu a chipani omwe adamovotera alemekezedwa. Zimenezinso zikumapatsa mphamvu chipani pa a phungu awo. Chachiwiri kunali kufuna kuletsa ndale za kabisalira pakati pa a phungu komanso kuwonetsetsa kuti pali chilungamo cheni cheni pochita zithu poyera.

Koma kusithaku sanagwirizane nako anthu ena powona mlandu omwe unali ku khoti pakati pa Wankulu wa Malamulo (Attorney General) ndi akulu akulu woyang'anira memene ndale zili kuyendera (PAC) zoti lamuloli sinayenera kukhudza mabungwe omwe anali kujnja kwa Nyunmba ya Malamulo chifukwa ati kutereko nkusokoneza. Khoti lidapeza kuti kusitha konseku kunali ndale basi chifukwa sanayenera kuphatikiza mabungwe akunja ai. Khoti lidapezanso kuti kusithaku mkwachilendo poyekeza ndi maiko ena pakhani yowolowekerayi ndipo zoterozo zingapangitse dziko la Malawi kukhala yekhayekha pa nkhani ya lamuloli. Khotili lidatinso pokhudza mabungwe a kunja kwa nyumba ya Malamulo kunali kufuna kuopsyeza a phungu omwe anali mu mabugwe a kunja kwa nyumbayi mabungwe omwe zolinga zawo ndi ugwiro.

Koma anthu amene anthirirapo ndemanga pa lamuloli, panali maganizo awiri, lina loti Lamuloli asasithe pamene ena anati lisithidwe. Amene amti lisasithidwe makamaka mafumu a dziko lonse anati zipani ndi zomwe zimapangitsa kuti munthu amusaskhe ku Nyumba ya Malamulo. Ndipo adati munthu kuchoka chipani chake nkulowa china mkusoneza anthu omwe adamusakha. Mafumu ananenetsa kuti phungu yemwe wachoka chipani chake nkulowa china ayenera kuchotsedwa ndipo chisakho chapadera chichitike kuti wina akalowe m'malo ake. Ngati adasakhidwa ngati woima payekha ayenera kuchotsedwanso kuti anthu asakhe wina m'malo mwake ndi a Bungwe la a phungu a maim u Nyumba ya Malamulo adavomereza fundoyi.

Pogwirizana ndi anzawo a Chipani cha Kongelesi adati mkosafunikira kumakambakamba khani ya ndime 65 chifukwa nkhani yidafotozedwa bwinobwino pa Ndime 62 (2) ya Malamulo oyendetsera dziko lino m'mene phungu ayenera kuchita poyimirira anthu a dera lake potengera m'mene Malamulo oyendetsera dziko lino anenera. Malamulo a Bungwe la Chisankho munthu akasakhidwa pansi pa chipani kapena pa yenkha ayenera kuti akhale chomcho osasitha mbali.

Mabungwe oyang'anira ufulu wa anthu adagwirizana nawo maganizo osasithanso Ndime 65ndipo adati ngati phungu afuna kusitha chipani ayenera kubwerera kwa anthu p[okachitanso voti. Iwo adati amene amkonza Malamulo oyendetsera dziko lino adafuna kuti pakhale mkhalidwe pakati pa a ndale nchifukwa chake adayikamo ndime ziwirizo 62 & 65. Pachifukwa chimenechi adachenjeza kuti ufulu wotha kulowa bungwe lomwe munthu afuna litsatane ndi Malamulo oyendetsera dziko lino potsata chikhulupiriro chomwe anthu ovota angakhale nacho pa a phungu awo. Iwo adati ufulu olakhula ndi kulowa bungwe lilonse munthu angafune liyenera kukhala ndi malire makamaka kuti Ndime 44(2) ya Malamulo oyendetsera dziko akutsatidwa.

Otsutsana ndi Lamuloli (ndime 65) amati lamuloli likungupatsa mphamvu zambiri zipani pomwe a phungu awo azikhala mu mpanipani. Pachifukwa chimenechi akuti zimapangitsa kuti a phungu asamapereke maganizo awo koma a zipani chifukwa choopa kuchotsedwa. Komanso akuti lamuloli likutsutsana ndi lamulo la ufulu wolowa kapena kukhala pa gulu monga Ndime 32 ya Malamulo oyendetsera dziko poopsyeza kuti muthu achotsedwa pa uphungu akalowa chipani kapena bungwe lina. Komanso likuopsyeza ufulu wochita nawo ndale monga Ndime 40 ya Malamulo oyendetsera dziko anenera. Iwo anachenjeza kuti sibwino kumangolola zofuna za aliyense. Iwo adanenetsa kuti cholingas cha ufulu wa demokalase nkuwonetsetsa kuti phung akuchita zithu zokomera dera lake.

### 3.4 Nthawi yokhalira pa udindo wa phungu wa kunyumba ya Malamulo.

Malamulo oyendetsera dziko ndi Malamulo a Chisankho cha a phungu ndi Pulezidenti akunenepo zomuyenreza munthu kuti asakhidwe phungu, momga chisankho chachipulula ndi chisankho chenicheni. Koma Malamulowa sakunenapo kathu pa za nthawi yomwe phungu angakhalire pa udindiwu. Chisankho chokha ndi chimene chinmganene kutalika kwa nthawi yomwe phungu angakhalire pa udindowu.

Pankhaniyi anthu ambiri adalakhulapo ndikupereka maganizo awo. Mwa zina anthuwa adti chisankho chokha sichiri kukwanira kunena nthawi yomwe phungu angakhalire pa udindowu ndiponso nkobvuta mwa njira yimeneyi kuti phungu amene sakuchita bwino achotsedwe chifukwa cha zinyengo komanso umphayi wa anthu omuvotera popeza amzolowera. Choncho anthuwa adati nkofunika kuti phungu

azisakhidwa maulendo awiri kuti potero azipereka mpata kwa anthu ena kuti askhidwenso. Ndipo zimenezi zingapatse mpata anthu ena kuti atengepo mbalai pa nkhani ya chitukuko cha dziko makamaka achinyamata.

Maganizowa anabvomerezedwa ndi ma Bungwe lomwe lmayang'anira za ufulu wa anthu la CHRR kuti nkoyenera kuti phungu akhale ndi malire pa udindowu monga momwe ziliri ndi udindo wa Pulezidenti popeza onsewa ndi osakhidwa ndi anthu kuti awatumikire.

Komabe ena sanagwirizane ndi fundo yimeneyi yoti phungu akhale ndi malilire yosakhidwa ku Nyumba ya Malamulo. Iwo akutim chisankho chimakwanira kuwona nthawi yomwe phungu angakhalire pa uphunguwu. Iwo adati sibwinpo kutaya nthawi ndikumakamba za nthawi yokhalirira phungu pa udindo wake koma chofunikas ndikuwona kukula kwa munthuyu (zaka za kubadwa) zomuyenereza kukhala phungu. Iwonso adaiti sibwino kuyerekeza ofesi ya Pulezidenti ndi ya phungu popeza ndi pulezidenti yenhkha amene angagwiritse ntchito phamvu zake molakwika kusiyana ndi phungu wa ku Nyumba ya Malamulo.

### 3.5 Zomuyenereza munthu kukhala phungu

Ndime 51 ya Malamulo oyendetsera dziko linopali ndondomeko zofotokoza zomuyenereza munthu kuti asakhidwe kuchita nawo chisankho cha uphungu wa kunyumba ya Malamulo. Mwa zina nkoyenera kuti munthu azitha kulakhula ndil kulemba chingelezi bwino lomwe ndi cholinga choti akathe kutengapo mbali mu zokambirana za ku Nyumba ya Malamaulo. Izi zikutathauza kuti palibe lamulo lenileni lofgotokoza za maphunziro omwe ayenera kukhala nawo kuti asakhidwe pa uphungu. Koma a Bungwe loyendetsa Chisankho m'dziko lino akuyendetsa lamuloli poonetsetsa kuti amene alibe satifiketi achite mayeso olemba ndi kuwerenga chingelezi.

Anthu ena tsono adati nkofunikas kuti nkhaniyi yiunkidwe bwino. Mwachitsanzo mafumu a mchigawo chapakati adati munthu ofuna kupikisana nawo pa mpando wa uphungu ayenera kukhala ndi Dipoloma yochokera ku Sukulu ya Ukachenjede ya Malawi ati poterepo Nyumba ya Malamulo idzakhala ndi a phungu okhwima nzeru. Ati iwowa adzatha kukambirana za nzeru ku Nyumba ya Malamulo zotukula dziko lino. A Bungwe loona za Malamulo (Law Society) ndi a Sukulu ya Ukachenjede adgwirizana nayo kwa thunthu fundoyi. Akutyi kutero kudzapangitsanso kuti achinyamata azilimbikira sukulu ndi cholinga choti adzathe kupikisana nawo pa udindo wa uphungu. Komabe ena adati Dipoloma ai koma Satifiketi ya Fomu Folo (MSCE) kapena yofanana nayo.

Mabungwe ena owona za ufulu wa anthu adati maphunziro a pamwamba sapanga munthu kukhala okhwima mu nzeru monga momwe zidawonekera pa misokhano ya a phungu posachedwapa kuti

a phungu ena ophunzira mkhalidwe wawo unali okhumudwitsa. Koma ena anakaika kuikapo maganizo awo ati poti achinyamata omwe anafika fomu folo amalephera kulemba ndi kuwerenga chingelezi bwino.

Magulu ena ankanitsitsa kwa ntu wa galu maganizo ofuna kuti at a phungu azikalakhula zilakhulo zathu momga Chichewa ku Nyumba ya Malamulo

### 3.6 Aphungu wogwira ntchito mophatikiza ngati Nduna

Iyi inalinso nkhani yomwe inabweretsa kusamvana (maphokoso?) chisanafike chaka cha 1997. Gawo 51 (2) (e) la m'buku la malamulo adziko lino amati "palibe yemwe adzatsankhidwe kukhala phungu wa nyumba ya malamulo ngati (e) iye akugwirizira kapenma ali pa udindo uli wonse wa boma……." Ndime iyi ikulingana ndi mfundo ina yofunika mmalamulo a ku Britain omwe adakhazikitsidwa zaka zikwi zapita ndi cholinga chowonetsetsa kuti nyumba ya malamulo siyikulamuliridwa ndi Mfumu (wa dziko la Britain). Koma ku Britain tsopano a phungu amtha kugwira ntchito ngati nduna za boma.

Mfundo yoti phungu asakhale nduma imatsatidwanso ndi anzathu monga a ku America komwe phungu sangasankhidwe kukhala nduna ya boma.

Pa chigamulo pa mlandu wa a Nseula ndi anzawo motsutsana ndi Mkulu wa Malamulo (Attorney General) ndi Chipani cha Malawi Congilesi a Jaji (Judge) a Mwaungulu adagamula kuti ngati phungu asankhidwa ngati nduna, ndiye kuti wasiya mpando wake wa kunyumba ya malamulo chifukwa cha ndime 63 (1) ya malamulo a dziko lino. Ndimeyi imafotokoza kuti phungu amatula pansi mpando wake ngati pali zoletsa zina zoti akanati iye si phungu sangamusankhe dala kukhala phungu. Monga tanenera poyamba Gawo 51 (2) (e) limaletsa kusankha munthu yemwe akugwira kale ntchito za boma kukhala phungu wa nyumba ya malamulo. Chigamulo cha Mwaunguluchi anachipanga potsatira mfundo yoti unduna ndi ntchito ya boma.

Koma a khoti lalikulu la Supulimu anatsutsa zomwe linalamula High Khoti ponena kuti unduna si ntchito ya boma koma ya ndale. A Khoti la Supulimu, lomwe ndi lomaliza pa mphamvu pa makhoti onse, anagamula motere potsatira gawo 75(2) ndi gawo 98(5) la malamulo lomwe limasiyanitsa ma udindo a phungu ndi nduna. A Khoti lomalizari anadaliranso chigamulo china chakale pa mlandu wa Mkulu wa Malamulo motsutsana ndi a Chipeta pomwe zidapezeka kuti Malamulo a dziko lino amapatsa mphamvu Pulezidenti kusankha nduna anthu omwe ndi aphungu komanso omwe Sali mnyumba ya malamulo.

Chigamulo china chomwe Khoti la Supulimu lidagwiritsa ntchito chidachoka pa mlandu wina wakale wa Pulezidenti wa dziko la Malawi ndi Sipikala motsutsana ndi R.B. Kachere. Pa mlanduwu a khoti anati Pulezidenti ndi Sipikala wa Nyumba ya Malamulo ndi ma udindo a ndale koma osati a ntchito ya boma. Kusintha kwa chigamulo cha khoti lomaliza la Supulimu pa mlandu wa a Nseula kunavomelera kusankha kwa a phungu kugwira ntchito ngati nduna za boma kusonyeza kuti Malamulo athu oyendetsera dziko atengera zinthu pang'ono kuchokera kwa azungu a ku Britain ndiponso zinthu zina pang'ono kuchokera ku dziko la Amerika.

Pokambirana pathu pa nkhaniyi ndi magulu a anthu m'midzi anthu ambiri amati momwe awonera m'mbuyomo zikuwoneka kuti njirayi siyabwino. Anthu adati aphungu asamasankhidwe kukhala nduna popeza uphungu ndi ntchito yayikulu payokha. Unduna umasokoneza aphungu kutumikira bwino anthu awo ku Konsitituwense. Komanso anthu anawona kuti kuphatikiza kwa maudindo awiri, uphungu ndi unduna, kukutsutsana ndi mfundo yofunika mmalamulo oyendetsera dziko yoti pakhale kusiyana pakati pa mbali zitatu za boma (boma, Nyumba ya Malamulo ndi makhoti). Mbali zitatu zabomazi zimayenera kuti iliyonse ikhale payokha ndi cholinga choti ziziwunikira kuti pakhale chilungamo ndi kukhulupirirana.

### 3.7 Sipikala wa nyumba ya malamulo

Gawo 53(1) limakhazikitsa ofesi ya Sipikala wa Nyumba ya Malamulo ndipo limati Sipikalayo asankhidwe ndi aphungu ochuluka mnyumbayo. Izi kawiri kawiri zimachitika pa msonkhano woyamba wa Nyumba ya Malamulo chikangotha chisankho cha Pulezidenti ndi aphungu. Apa zikuwonekeratu kuti zowayenereza amene akufuna kukhala phungu ndi zofanana ndi zowayenereza omwe angafune kuyima ngati Sipikala ku Nyumba ya Malamulo.

Anthu okhuzidwa adati pozindikira kufunika ndi kukula kwa udindo wa Sipikala nkofunika kuti munthu wokhala pa udindowu azikhala wodziimira payekha. Kuti izi zitheke, mabungwe wolimbikitsa za ufulu wa anthu adati nkofunika kuti malamulo woyendetsera dziko aletse pulezidenti kukhala ndi mphamvu zomuchotsa Sipikaka pa mpando chifukwa izi zitha kubweretsa zachinyengo ndipo ndi zotsutsana ndi kuzidalira kapena kuyima pa yekha kwa Nyumba ya Malamulo ndi Sipikala. Choncho udindo wa Sipikala ndi wofunika kuti ukhale wa mphamvu zofanana ndi ma udindo a wa mkulu wa za malamulo (Chief Justice) ndi Wachiwiri kw Pulezidenti (Vice President).

Anthu adagwirizananso kuti phungu kuti asankhidwe ngati Sipikala kapena wamkulu wa Nyumba ya Malamulo nkofunika

kuti akhale wakhala ali phungu kosachepera zaka zisanu. Apa akuchitira kuti phungu yemwe asankhidwe kukhala Sipikala azikhala wodziwa bwino zochtika ku nyumba ya malamulo kuti atsogolere bwino aphungu mnyumbayo.

Maganizo ena omwe adabwera mukukambirana ndi bungwe loyimira maloya (akatswiri a malamulo) la Malawi Law Society ndi loti pafunika kukhazikitsa mfundo mmalamulo woyendetsera dziko lino kufunika koti mpando wa Sipikala udzikhalabe ngakhale Nyumba ya Malamulo atayithetsa kuti Sipikala wakale azigwira ntchito mpaka Sipikala wina atasankhidwa ndi nyumba ya Malamulo. Pokwaniritsa mfundo yotere nkofunika kuti phungu yemwe wasankhidwa kukhala Sipikala adzitula pansi udindo wake wa chipani ndi cholinga choti athe kugwira ntchito ya u Sipikala mosakondera aliyense kapena chipani chilichonse. Anthu adati izi zidzalimbikitsa mfundo yomwe ili mmalamulo woyendetsera dziko yoti magawo atatu aboma azikhala woyima pawokha. Izi zidzalimbikitsa udindo wa Sipikala ndi kupangitsa kuti Sipikala asachotsedwe wamba ndi kusankhidwa ngati nduna ya boma ngati momwe zinachitika m'boma lapita lija.

Misonkhano inati ngati mfundoyi angayibvomereze malamulo oyendetsera dziko lino akufunikanso kuti afotokoze mwa mvemvemve zinthu zomwe zingachititse Sipikala kuchotsetsa pa mpando wake ndi aphungu osachepera matheka awiri a nyumba ya malamulo (two thirds majority). Izi zidzateteza ndi kulimbikitsa mpando wa Sipikala kuti aphungu asathe kuchotsa Sipikala popanda zifukwa zenizeni.

## 3.8 ZINZ NDI ZINA

### 3.8.1 Aphungu Kudulira Chisamani Nyumba ya Malamulo

Pa sonkhano wina wa bungwe la a phungu achizimayi m'nyumba ya malamulo anthu anadandaula kuti m'khalidwe womwe wabwera posachedwapa pomwe aphungu akumathamangira ku khoti kukadulira chisamani kapena kukasumila Nyumba ya Malamulo ngati sadakhutire ndi mfundo zomwe agiwirizana mnyumbayo zikusokoneza kayendedwe ka Nyumba ya Malamulo. Apa aphungu achizimayi adati mpofunika kuti aphungu onse azigwirizana chimodzi ndipo kuti phungu asamloledwe kutsutsa zomwe Nyumba ya Malamulo yamanga. Iwo anati aphungu azigwira ntchito limodzi ndipo pasamapezeke ena otsutsana ndi maganizo agulu popeza izi zikupeputsa mphamvu ndi ulemu wa nyumba ya malamulo.

### 3.8.2 Kuyitanitsa Msonkhano wa Aphungu

Nkhani ya mphamvu za Sipikala wa Nyumba ya Malamulo anayikambanso pa msonkhano wa bungwe la a phungu a chizimayiwa. Iwo sadagwirizane ndi gawo 59 la malamulo woyendetsera dziko lino lomwe limati Sipikala angathe kuyitaitsa msonkhano wa a phungu pokhapokha atakambirana ndi a Pulezidenti chifukwa iwonso ndi Phungu wa Nyumba ya Malamulo. Ena adati izi zikumabwezeretsa m'mbuyo ntchtio ya Nyumba ya Malamulo popeza a Pulezidenti atha kukaniza kuti aphungu asakumane pamene iwo akufuna kutero. Enanso anati kupempha chilolezo kwa Pulezidenti kukuphwanya ufulu wa Nyumba ya Malamulo kuti ikhale yoziyimila payokha. Motero aphungu adapempha kuti mfundo yoti Sipikala adzipempha chilolezo kapena kukambirana ndi Pulezidenti asayitanitse msonkhano wa aphungu ichoke.

Koma aboma analimbikira kutsutsana ndi zimenezi ponena kuti zinthu zikhale momwe zinaliri. A boma adati ali ndi udindo woyendetsa ndi kuyang'anira kayendetsedwe ka chuma mdziko muno. (Msonkhano wa aphungu a Nyumba ya Malamulo umafuna ndalama zambiri nthawi zonse).

# CHIGAWO CHACHINAYI

## 4. ZISANKHO

### 4.1 Bungwe loyang’anira ndi Kuchititsa Zisankho

#### 4.1.1 Mkulu wa bungwe loyang’anira zisankho

Ndime 75(1) limati mkulu wa bungwe loyendetsa chisankho chisankho la Malawi Electoral Commission ayenera kukhala jaji yemwe adzasankhidwa ndi Pulezidenti potsatira kuvomereza kwa bungwe loyang’anira oweruza milandu la Judicial Service Commission. Choncho ndi majaji okha omwe angakhale pa udindo wa wamkulu wa bungwe loyang’anira ndi kuchititsa zisankho mdziko lino.

Misonkhano yokambirana ndi anthu yambiri idasonyeza kuti anthu ambiri sakugwirirzana ndi momwe zinthu zirili pano kuti majaji okha ndi amene angakhale wa mkulu wa bungwe loyang’anira ndi kuchititsa zisankho. Poyamba anthu adati zifukwa zosankhira majaji pa udindowu zikutsutsana ndi zomwe zachitika mmbuoymu pamene anthu akhala wokaika ndi wosakhutira ndi umo majaji omwe akhala akulu abungwe loyang’anira zisankho akhala akugwirira ntchito yawo, mokondera mbali zina. Kachiwiri, anthu awona kuti pakhoza kukhala povuta pang’ono kuti majaji ena agamule mosakondera pa milandu yokhudza bungwe loyendetsa zisankho ncholinga chofuna kuteteza jaji mzawo. Kachitatu, anthu ena okhudzidwa adati akatswiri a malamulo (maloya) nthawi zambiri satha kuyendetsa bwino zinthu ndipo popeza ntchito yayikulu ya bungwe lochititsa zisankho ndi kuyendetsa bwino zinthu zokhudzana ndi chisankho, maloya sangakwaniritse kuchita izi. Anthu adati choncho nkofunika kuti poganizira kusankha munthu pa udindo wa mkulu wa bungwe loyendetsa zisankho nkhani yeniyeni ikhale kuti munthuyo akhale wodziwa nthcito ndi wokhulupirika koma azikhala woti ali ndi maphunziro ena ali onse aukachenjede. (First Degree)

Koma anthu ena adati zinthu zikhale momwemu popeza mposavuta kudziwa kukhulupirika kwa majaji chifukwa cha cha udindo wawo. Ena anatinso mwina loya aliyense ngakhale asali jaji atha kumusankha kukhala mkulu wa bungwe lochititsa zisankho ndi cholinga choti adzitha kutsatira bwino milandu yokhudzana ndi kusamvana pa zotsatira za zisankho.

### 4.1.2 Anthu oyenera kusankhidwa kukhala m'bungwe loyendetsa chisankho

Malamulo oyendetsera dziko lino ndime 75(1) akuti bungwe loyang'anira ndi kuchititsa zisankho la Malawi Electoral Commission likuyenera kukhala ndi Mkulu wa bungweli ndi anthu ena (mamembala) osachepera asanu ndi m'modzi (6) omwe adzasankhidwa motsatira zomwe yakhazikitsa nyumba ya malamulo pa nkhaniyi. Apa likukamba za Malawi Electoral Commission Act yomwe imati Pulezidenti atha kusankha anthu kukhala mamembala abungwe lochititsa zisankho atakambirana ndi kugwirizana ndi atsogoleri a zipani zonse zomwe ziri ndi aphungu m'nyumba ya malamulo. Choncho m'mbuyomu izi zapangitsa kuti anthu ochokera mzipani zosiyana asankhidwe kukhala makomishonala a Electoral Commission.

Chiyambire chaka cha 1994 ma Komishonala kapena mamembala a bungwe loyang'anira ndi kuchititsa zisankho akhala akuchokera kuzipani za UDF, MCP ndi AFORD. Ngakhale kuti lero pali zipani zisanu ndi zitatu mu nyumba ya malamulo, ma membala a bungweli adakali ochokera ku zipani zitatu zomwezi.

Mpofunika kumvetsa kuti kutanthauza kwenikweni kwa mfundo ya Lamulo Lokhudza Bungwe Loyendetsa Zisankho (Electoral Commission Act) sinali kuti makomishonala adzikhala okhawo ochokera mzipani zomwe ziri ndi mipando yochuluka ku nyumba ya malamuloyi. Cholinga cha mfundo yoti Pulezidenti azikambirana ndi atsogoleri a zipani zomwe zili ndi aphungu ambiri chinali choti okhawo ali ovomerezeka asankhidwe kukhala makomishonala a bungwe lochititsa zisankho. Koma zomwe zakhala zikuchitika m'mbuyomu zikhala zotsutsana ndi iz ndipo anthu akhala okhumudwa ndi osakhutira ndi wanthu amene asankhidwa kukhala makomishonala. Mwachitsanzo, mafumu anena kuti sakugwirizana ndi mfundo yoti andale okha ndiye adzikhala makomishonala ndipo iwo ati anthu a m'mabungwe wolimbikitsa ufulu wa a anthu adzithanso kusankhidwa kuti aziyendetsa nawo bungwe lochititsa zisankho ncholinga cholimbikitsa kuti bungweli likhale loyima palokha. Anthunso anatsutsana ndi zodalira anthu andale ponena kuti andalewo alibe ukadaulo ndi zowayenereza zina kuti azitha kuwongolera bwino bungwe lochititsa chisankho.

Pamsonkhano wina ndi anthu okhudzidwa ndi nkhaniyi ku Blantyre anthu adanena kuti mwina nkofunika kuti

mamembala woyang'anira bungwe lochititsa zisankho asamakhale atsogoleri andale koma anthu ena odziwa ntchito zotere. Koma izi adadzitsutsa anthu pamsonkhano wina ponena kutianthu andale sipoyenera kuwachotseratu pankhani zokhudzana ndi zisankho ncholinga choti adzitha kuvomereza msanga zotsatira za zisankho popeza andale ndiye eni zisankhozo. Koma anthu ena adangoti nkofunika kusintha nkhani ya makomishonala woyang'anira bungwe lochititsa zisankho koma sadafotokoze bwino momwe izi zingayendere.

### 4.1.3 Ntchito a bungwe loyendetsa chisankho

Mwazina bungwe loyang'anira ndi kuchititsa zisankho liri ndi mphamve (zochokera mmalamulo woyendetsera dziko ndi nyumba ya malamulo la Electoral Commission Act) yonena kuti kukhala makonsitituwense kapena aphungu angati pa chisankho ndiponso kugawa malire a makonsitituwensewo kapena kuti malire a dela la phungu aliyense.

Anthu okhudzidwa ndi nkhaniyi adasonyeza kusakhutira ndi momwe bungweli lakhala likugawa malire a makonsitituwense (dela la phungu). Mafumu ambiri ndi wodandaula kuti samafunsidwa bungweli likamagawa malire a madela a phunguwo.

Anthu a mmabungwe wolimbikitsa ufulu ati mwina kungakhale kwabwino boma litakhazikitsa bungwe lina kuti liziyang'anira zogawa malire a madela a phungu ndipo kuti bungweli lidzidzayenera kukambirana ndi anthu onse ofunikira lisadagawe malire a dela la phungu. A mabungwe wolimbikitsa ufuluwa adati izi zitha kuchepetsa andale kuchita za chinyengo ncholinga chowonjezera mphamvu zawo pochulukitsa chiwerengero cha aphungu. Ndipo iwo adapitiriza kunena kuti nkofunika kuti malamulo oyendetsera dziko atchule nambala ya aphungu ndi madela awo mMalawi muno ncholinga choti chiwengero cha aphungu chisamangokwezedwa wamba pofuna kuwonjezera mphamvu za ndale. Iwo adatinso izi zingathandize kuchepetsa ntchito ya bungwe loyang'anira ndi kuchititsa zisankho kuti lidzilimbikira zophunzitsa anthu momwe angaponyere voti.

Koma a bungwe loyimirira maloya la Malawi Law Society ndi a ku univesite ya Malawi adakamba zosiyana ndi izi. Iwo adati bungwe loyang'anira ndi kuchititsa zisankho litakhala kuti ndi loyimadi palokha pokhala ndi

makomishonala ena oti siandale sikofunika kukhazikitsa bungwe lina loti lidzigawa malire a madela a aphungu.

## 4.2 Mitundu ya Chisankho

### 4.2.1 Kuchuluka kwa Anthu Posankha Pulezidenti

Gawo 80 (2) la malamulo woyendetsera dziko limati Pulezidenti adzasankhidwa ndi anthu ambiri pachisankho. Mawu oti “anthu ambiri oponya voti” abweretsa kusamvana kwambiri mmbuyomu kuno ku Malawi. Poyamba penipeni liwu loti “ambiri” ndi lovuta kulitanthauzira kodi izi zitanthauza kuti yemwe wapeza mavoti ambiri kuposa ena onse kapena yekhayo wapeza mavoti wopitirira theka la anthu onse oponya voti (50 percent)?

Kachiwiri nkhani yikuvuta ndi tanthauzo la “anthu oponya voti” mmalamulo woyendetsera dziko lathu. “Anthu oponya voti” ndi anthu onse oyenerezeka kuponya voti. Choncho tanthauzo lenileni la “anthu ambiri oponya voti” likhoza kukhala kuchuluka kwa “anthu oyenerezeka kuponya voti” posalingalira ngati iwo aponya voti kapena ayi.

Pa mulandu womwe a “Gwanda Chakuamba ndi ena motsutsana ndi Mkulu wa Malamulo ndi ena”, a Chakuamba adatsutsana ndi zotsatira za zisankho za 1999 ponena kuti yemwe adapambana pa chisankhochi sadapeze mavoti omuyenereza kukhala Pulezidenti ngati momwe ikufotokozera gao 80 (2) la malamulo woyendetsera dziko lino. Iwo adati wopambanayo amayenera kupeza mavoti wopitirira theka la anthu onse omwe adaponya voti (50+1 percent). A Chakuamba ndi ena antinso gawo 96 (5) la ndondomeko zoyendetsela chisankho cha Pulezidenti ndi aphungu (Parliamentary and Presidential Elections Act) likutsutsana ndi malamulo woyendetsela dziko lino chifukwa silikugwirizana ndi gawo 80 (2) la malamulowa. Iwo amatengeranso kutsutsa kwao pa gawo lachisanu (5) la malamulo woyendetsera dziko lino.

Koma a khoti mchigamulo chawo adati mawu oti “anthu ambiri oponya voti” akutanthauza mwachidule “anthu oponya voti opitirira omwe wopikisana wina wapeza”. A khotiwa adapanga chigamulochi atayang’anitsitsa ndime zina za malamulo woyendetsera dziko lino zomwe zikukambapo

zosankha anthu pa maudindo osiyanasiyana monga magawo 49 (2), 53 (1) ndi (73 (3).

Khoti lidatinso ngakhale pali mau oti “anthu oyenera ku vota” mu Malamulo oyendetsera dziko lino mauwa akutathauza anthu okhawo amene amaponya voti. Ndipo kutanganidwa ndi kuona matathauzo a mau ena kungangosokoneza zithu pa zifukwa zinagapo; Choyamba munthu saumilizidwa kukavota mu Malawi muno choncho si onse amene ali nkaundula wa voti omwe amakavota pachifukwachi siambiri omwe ali mu kaundula omwe amakaponya voti

Komanso m’Malamulo oyendetsera dziko lino sanenapo kathu pa zomwe zingachitike kwa munthu opikisana nawo yemwe sakukwanitsa nambala yofunikira. Pachifukwa chimenechi nkofunika kuona kuti zithu kodi chisankho chachibwereza chichitike nthawi yanji, ndipo ayenra kupikisana nawo ndani, ndi nthawi yosankha opikisana nawo ndi zofunika kuziunika bwinobwino. Khoti lidatinso:

Malamulo oyendetsera dziko lino adalembedwa mozama komanso moyanga’anira zithu zambiri choncho munthun akafuna kumasulila Malamulowa nkofunika kutero modekha osangoti chifukwa ndidapita ku Sukulu ya za Malamulo. Pa chifukwa chimenechi pofuna kulemab Choncho kalembedwe ka Malamulo amenewa sikofunika kungolemba mwa bwatbwat phulu ai koma monzama kwambiri ndi cholinga choti zolinga za Nyumba ya Malamulo zikwaniritsidwe.

Kutathauza kwa a Malamulo pa Malamulo oyendetsera dziko lino amati pulezidenti amsakhidwa akapeza mavoti okwanira kusiyana ndi ena. Pachifukwa pa Chisankho cha 2004 adsakhidwa ndi mavoti okwana 34% mwa mavoti onse amene anaponyedwa.

Anthu ambiri aperekapo magnizo awo pokhudza Lamuloli. Ambiri akuti Pulezidenti azisankhidwa ndi anthu osachepera theka la anthu omwe avota kuwonetsa kuti alidi ndi ulamulilo ndi mphamvu zotha kulamulila. M’mau ena ndiye kuti ulamulilo umayenda bwino ngati pali kuvomereza kochokera kwa anthu ambiri. Msokhano wa Bungwe lowona za Malamulo ndi Sukulu ya Ukachenjede ya Malawi udati zoterezi ndi zimene zingapatse chikhulupiriro kwa anthu mwa munthu amene wasakhidwa. Mabungwe owona za ufulu a zipembedzo and a ndale adgwirizan nazo ndipo adati ngati pachisankho mnthu alemphera kukwaniritsa theka la mavoti ndi anthu awiri amene akupikisana kwambiri pa mavoti ayenera kupikisanaso kachiwiri kuti paoneke wopambana weniweni.

Kachiwiri adati monga udalili Mlandu wa a Chakuwamba munthu amene ayenera kupambana pa chisankho ndi yekhayo amene ali ndi mavoti ambiri makamaka osachepera theka la mavoti onse. Maganizo maenewa anavomerezedwanso ndi mafumu a mzigawo zones zitztu. A

Bungwe la a phungu a chimai ku Nyumba ya Malamulo dagwirizana nayo fundoyi. Anthuwa adati kupanda kutero kungakhale kulakwira ntundu wa a Malawi poganizira kuti ndalama za chisankho timadalirira mabungwe ndi maiko akufuna kwabwino malingana ndi uphawi umene uli mdziko muno. Zithu monga chinyengo ndi ziphuphu ndi zina mwa zithu zomwe zingapangitse Bungwe la Chisankho kupangitsa chisankho cha chibwereza cha pulezidenti.

Kachitatu anthu adati Malawi yitenge njira yosankha Pulezidenti ku chipani chomwe chapeza a phungu ambiri. Izi zingapangitse kuti Pulezidenti akhale ndi anthu omutsatira ambiri mu Nyumba ya Malamulo komanso m'dziko.

Pansokhano omwe udachitikira ku Mpoto pakati pa ma Bungwe owona ufulu wa anthu, a zipembedzo, akuluakul a zamaphunziro ndi akatswiri ena adwonjezerapo maganizo a chinayi pa kasakhidwe ka Pulezidenti. Adati, poonjezera kuchuluka kwa mavoti kuti Pulezidenti asakhidwe, anati nkufunika kuti apezenso mavoti okwana mu mzigawo ndi m'maboma kusonyeza kuti wa bvomerezedwa ndi ntundu wonse wa a Malawi. Izi zingachepetse kukhala ndi Pulezindenti ochuka m'chigawo chimodzi pa ndale chifukwa cha ntundu wake.

### 4.2.2 Njira yosankhira phungu wa ku Nyumba ya Malamulo.

Anthu ena adati kasankhidwe ka a phungu a ku Nyumba ya Malamulo azichokera ku zipani potsata m'mene chipani chapezera mavoti pa chisankho. Ati njira imeneyi ingathandize kuti zingapangitse kutyi anthu obvutika ndi awo alipo ochepa a khale ndi owaqyimirira ku Nyumba ya Malamulo monga amai ndi anthu olumala chifukwa chipani chimasakha a phungu mu Nyumba ya Malamulo chsakho chitatha. Adatinso fundoyi ingathandize kuti pasamakhale kusakaza ndalama pomachita zisakho zapadera pamene phungu wasiya ntchito yake popeza chipani chizikangosankha wina phungu opanda kuchita chisankho.

Koma anthu ena anati njirayi singagwire ntchito bwino kuno ku Malawi chifukwa ingapatse mpata atsogoleri azipani kukhal;a ndi ulamulilo wa khanza pa anthu awo.

Pa nkhani yomweyi anthu ena anati pofuna kuti amai mu Nyumba ya Malamulo a chuluke kufika pa 30% nkofunika kuti papezeke njira yoti amai azikhala theka la theka (1/4) la aphungu M'nyumba ya Malamulo.

### 4.2.3 Chisankho cha pulezidenti ndi aphungu

Ndime 67 ya Malamulo oyendetsera dziko yikuti Chisankhu chizichitika Lachiwiri lililonso Msabata lachitatu la mwezi wa Mayi pakapita zaka zisanu zilizonse. Ngati izi sizingatheke chisakho chidzachitika tsiku lina lirilonse kuchokera pa tsiku Lachiwiriro koma pasanapite masiku asanu ndi awiri, ndipo tsikulo adzsakhe ndi a Bungwe loona za Chisakho.

Ndime 80 (1) ikunena kuti chisankho cha Pulezidenti chidzachitikira pamodzi ndi chisanlho cha a phungu a ku Nyumba ya Malamulo.

Zambiri zanenedwa malingana ndi m'mene chisakhochi chimayendera. Choyambirira akuti masiku ochitira chisankhochi a funika kusithidwa chifukwa choti chisakhochi chimachitika nthawi ya vula choncho misokhano yokopa anthu siyenda bwino komanso anthu amatanganidwa chifukwa ndi nthawi yolima. Komanso anati kuchita chisakho mu Mayi kutathauza kuchita chisakho kumapeto kwa chaka cha ndalama chomwe chingasokoneze nkhani ya chuma. Anthu ena akuti kutchula dzina la chisankho nkongousokoneza chabe akadangoti chisankhom chidzachitika pa mwezi wachitatu wa chaka.

Komanso adati nkofunika kuti zisakhozi azichita zones zitatu; Cha Pulezidenti, a phungu a ku Nyumba ya Malamulo ndi cha Makasala kupewa kusakanza ndalama zambiri.

Kachitatu anati chikatha chisankho nkofunika kuti misokhani yokopa anthu izletsedwa kuti Boma lizitanganidwa ndi ntchito yotukula dziko.

Kachinayi, kayendetsedwe ka chisankho anthu ambiri sakukawona bwino chifukwa kamakondera chipani cholamula chifukwa choti amakhala ndi zonse zowayenereza pa chisakho. Akuti njirayi ndi yabwino kwa maiko amene ndi okwera kale koma zipani zimakhala ndi ndalama zikwanira. Ena nati mu Africa nkobvuta kuti ena atenge boma chifukwa chipani cholamula chimakhala ndi zonse zowayenereza komanso amchita izi mosatsata malamulo. Izi zimapangitsa kuti chisankho chisayende bwino ndipo anthu amalephera kusakha boma la kumtima kwawo.

Pa chifukwa chimenechi nkoyenerta kuti pa nthawi ya chisankho pasmakhale boma lolamula ndipo nthawi yimeneyi amene azilamulira a khale a bungwe La pulezidenti (Presidential Council) momwe muzikhala atsogoleri onse azipani motsogozedwa ndi Mkhala pa Mpando. Wapampando azisithana mwenzi ndi mwezi ndi fundo za bungwe azipangira pamodzi osati palakeplake.

### 4.2.4 Nthawi yolengezera zotsatira za zisankho.

Nkhani yimeneyi imayendetsedwa ndi Lamulo Chisankho cha Pulezidenti ndi a phungu a Nyumba ya Malamulo. Potsata Ndime 99 ya Malamulo oyendetsera dziko, zotsatira za chisankho ziyenera kulembedwa mu Gazeti ya Boma ndi kulengezetsa pa wailesi ndi mnyuzi pepala yomwe yimatuluka tsiku lililonse m'Malawi muno patangotha masiku asanu ndi atatu chitachitikaq chisakho koma osadutsa maola makumi anayi ndi phambu zisanu ndi zitatau (48) nthawi yimene atsiliza kuwerenga zotsatira za chisankho.

Pa misokhano ndi mabungwe owona ufulu wa anthu ku Blantyre anthu adati nkofunika kuti zotsatira zizilengezedwa patapita masiku asanu ndi

awiri kuti anthu azikhala atatsiriza kufufuza zolakwika ndi mkulu woyendetsa chisakho muBoma lawo. Iwo adati chinachilichonse chobwera pa mbuyo pa masiku asanu ndi awiri chidzatengedwa ngati chithu chofuna kusokoneza zotsatira za chisankho.

### 4.2.5 Oyenera kuponya voti

Ndime 77 ya mu Malamulo oyendetsera dziko akuti aliyense ndi wololedwa kuchita nawo vote ya Pulezidenti, ya Makasala, ya a phungu ngakhale ya yofufuza maganizo a anthu (referendum) malingana ngati angakwanitse zimuyenereza. Chimodzi chomuyenereza munthu kuti avote ndi kuti akhale woti wakwanitsa zaka zakubadwa pa tsiku lo lembetsera mkaundula wa voti zokwana khumi ndi phambu zisanu ndi zitatu (18).

Maganizo a wean akuti nkhani ya zakayi azitengera tsiku lovotera osati lolembetsera mu kaundula chifukwa zimenezi zimalepheretsa munthu amene wakwanitsa zaka 18 patsiku lovota chifukwa choti amakhala mulibe mukaundula wa voti.

### 4.2.6 Chisankho chapadera

Ndime 44 ya Malamulo oyendetsera dziko pokhudzana ndi chisakho cha Pulezidenti ndi a phungu a ku Nyumba ya Malamulo akupereka zofunikira kuchita pa nthawi imene pakufunika chisankho cha padera, Chisankho chapaderachi chingachitike ngati phungu asiya uphungu kapena chifukwa cha imfa ya phungu.

Anthun adati mkofunika kuti nkhani ya chisankho chapadera ndiyofunika kuti yilembedwe mu Malamulo oyendetsera dziko. Akutinso amene angapikisane nawo pa chisanlho cha paderachi ndiwokhawo amene adapikisana nawo pa nthawi ya chisankho chachikulu popeza chisankho chapaderachi ndi mbali yimodzi ya chisankho choyamba.

## 4.3 Zina ndi zina

### 4.3.1 Kuunikanso Malamulo a Chisankho.

Anthu osiyanasiyana adagwirizana kuti nkoyenera kuti Malamulo a Chisankho awunikidwenso bwino kuti pakhale kufanana pakati pa chipani cholamula ndi zipani zina zotsutsa Boma komanso kuopa kuti chipani cholamula chisamapanirire zipangizo za Boma pa nthawi ya chisankho.

# MUTU 5

## 5. NTHAMBI YA BOMA YOLAMULA (EXECUTIVE)

### 5.1 Kulumbiritsa Pulezidenti kapena Wachiwiri Wake

Ndime 81(3) ya malamulo imayenereza osankhidwa pa mpando wa u Pulezidenti kulumbiritsidwa kuyamba ntchito yake pasanathe masiku makumi atatu (30) chimusankhireni. Palibe mlingo wa masiku pamene Pulezidenti ayenera kuyambira ntchito yake. Choncho Pulezidenti opuma ayenera kupitiriza ntchito mpaka Pulezidenti watsopano atalumbiritsidwa.

Pafupifupi pamisonkano yonse, anthu anaonetsa kusakhutirra ndi kupanda mlingo wa masiku pamene Pulezidenti asanalumbire makamaka potsatira zomwe zinachitika mchaka cha 2004 pachisankho cha Pulezidenti. Komabe nthumwi zinati sikoyenera kupitirira Pulezidenti asanalumbire. Mwa chitsanzo, mafumu a chigawo cha kumpoto anawona kuti kupitiriza masiku ponena kuti awunike madandaulo ndi kutsimikizira zotsatira kungabweretse zinthu zina zosakhala bwino. Komanso kutalika kwa nthawi yodikira kungayambitse ziwawa chifukwa chakuti mitima ya anthu imakhala m'mwamba pa nyengoyi.

Pemenepa nthumwi zinagwirizana kuti nyengo (nthawi) yodikira idzikhala kuchokera pakati pa masiku khumi ndi anayi (14 mpaka makumi atatu (30). Izi zidzathandiza kupereka ndikulandira ntchito ya u Pulezidenti mwa dongosolo. Komanso izi zidzathandiza kuunika boma lopuma ndi cholinga chofuna kuchepetsa kuonongeka kwa kwa chuma cha boma. Chinanso ndi chakuti bungwe la zachisankho ndi a makhoti adzatha kuunika madandaulo onse omwe apezeka panthawi ya chisankho. Apa nthumwi zinaona kuti nei koyenera kukhazikitsa nthawi yoyenera mu malamulo kuti akhoti adzitha kukhala ndi nthawi yoyenera kuti azithana ndi zidandaulo zonse zopezeka pa nthawi ya chisankho.

Panaganiziridwanso kuti nthawi yoyembekezerayi isamapitirire masiku makumi asanu ndi limodzi (60). Panaganiziridwanso kuti padzikhala ndondomeko zoyenera kuonetsetsa kuti Pulezidenti opuma asapange zinthu zosayenera kuthandiza kusintha udindo moyenera. Ena anaonanso kuti tsiku lolumbiritsa Pulezidenti lidzitchulidwa momveka bwione mumalamulo a dziko lino momwe limachitira ndi tsiku la chisankho.

Pazokambirana za mlingo wa masinku oyenera kudikira Pulezidenti asanalumbiritsidwe, zinthu zina zinaunuikidwanso monga kodi nthawi imeneyi idzikhala yoti Pulezidenti wopuma ntchito yake yatha kapena ayi. Zinaonedwa kuti ngati pazikhala

kuti nthawi yake yatha, ndiye kuti kuzikhala kuphwanya malamulo chifukwa adzikhala akupitiriza kugwira ntchito kupyolera momwe buku lamalamulo limanenera. Apa zinaganiziridwa kuti makumi atatu (30) adzikhala masiku omwe Pulezidenti wa pampando adzikhala akugwirabe ntchito podikira tsiku lake lomwe ayenera kupuma.

## 5.2 Zomuyenereza Munthu kukhala Pulezidenti Kapena Wachiwiri kwa pulezidenti

Zoyenereza munthu pa mpando wa Pulezidenti kapena wachiwiri wake zikupezeka pa ndime 80(6) YA MALAMULO. Ndimeyi ikuti oyenera kukhala pa mipando iwiriyi ayenera kukhala Mbadwiri kapena Mzika ya dziko la Malawi komanso akhale kuti wakwanitsa zaka makumi atatu ndi mphambu zisanu (35) zakubadwa.

Maganizo osiyanasiyana anaperekedwa pa mutu umenewu makamaka pankhani ya zaka. Ena amati zaka za munthu ofuna kuyima nawo u Pulezidenti zizikhala za pakati pa makumi atatu ndi mphambu zinau (35 kuthera pa makumi asanu ndi awiri (70). Ena anati kukhazikitsa zaka zomaliza za 70 zingathandize kagwiridwe ka tchito chifukwa udindo wa u Pulezidenti ndi olemetsa komanso umafuna luntha ndi nyonga. Koma mafumu achigawo chapakati adati zaka za mmunsi ndizofunika kukweza kufika pa makumi anayi (40) ndipo kuti pasakhale malekezero kutsogolo chifukwa chakuti munthu akamakula nzerunso zimachuluka. Apa anati pali zitsanzo zambiri kuti munthu opitiriza zaka 40 amakhala kuti wakhwima komanso ali ndi luntha loti akhonza kukhala Pulezidenti.
Nkhani ina inalinso ya maphunziro pamene anthu ambiri anagwirizana zoti setifiketi ya ukadaulo (Digiri ya ku Univesite) ikhale yomuyenereza munthu kuyima pa mpando wa u Pulezidenti. Apa nthumwi zinati munthu ofuna udindo wa u Pulezidenti adzikhala okonzeka kuthandiza pachitukuko cha dziko lathu komanso kuthandizapo pa ntchito pa dziko lonse mwa luntha ndi ukadaulo. Komanso panaonekanso kuti munthu wa maphunziro apamwamba angathe kumalamulira motsata malamulo bwino lomwe. China ndi chakuti ana adzikhala ndi chidwi cholimbikira maphunziro pofuna kuti adzakhale mtsogoleri wa dziko.

Ena anaona kuti ndi Pulezidenti kuti adzikhala ndi digiri ya u dokotala (Doctorate Degree) pochepetsa nkhalidwe lofuna kupeza madigiri mwa mseri pofuna kuti adzifanana ndi atsogoleri amayiko ena monga zakhalira mmbuyomu.

Chinanso chomwe chinaunikidwa pa misonkhanoyi chinali khalidwe la amene akufuna kudzayima namwo pa chisankho cha Pulezidenti. Nthumwi zinaona kuti munthu ofuna kauyima

pa mpandowu asakhale ndi mbiri iliyonse yakuba kapena kupezeka ndi mlandu wamtundu wina waqke uli wonse, kapena kunangiwa kumene. Ena amati aliyense opezeka ndi mlandu kapena kumangidwa ayenera kusavomerezedwa mosakambirana kupikisana nawo. Zinakambidwa kuti Ofesi ya Pulezidenti ndi yayikulu kwambiri mdziko muno, komanso ya wachiwiri kwa Pulezidenti ndi ya chiwiri kwa yaikulu kotero nkofunika dongosolo loyenera. Apa kunaganiziridwa kuti ndime 80(7) ya malamulo ayisinthe.

Nkhani ina yomwe inatuluka pa zokambirana ndi yokhudza chuma chomwe munthu ofuna kupikisana pa mpando wa u Pulezidenti ali nacho. Mafumu achigawo cha ku mmwera anaona kuti chuma chomwe munthuyu ali nacho chikhale gawo limodzi limodzi lomwe lingamuyenereze kuloledwa kupikisana nawo. Kotero ndikofunika kukhazikitsa mulingo wa chuma mu malamulo a dziko lino omwe angamuyenereze munthu kupikisana nawo pa u Pulezidenti. Apa anti izi zikhoza kuthetsa mavuto omwe alipo pano omagwiritsa ntchito mpando pofunan kudzilemeretsa. Kotero ndikofunika kuti onse ofuna kupikisaka pa u Pulezidenti adzineneratu za chuma chomwe ali nacho asanatero.

## 5.3 Ofesi ya Wachiwiri woyamba kwa Pulezidenti

Ndime 80 (4) ya malamulo imati wachiwiri oyamba wa Pulezidenti adzisankhidwa limodzi ndi Pulezidenti. Kotero dzina la wachiwiri oyamba wa Pulezidenti lidzikhala nawo pachipepala chovotera mmene limakhalira dzina la Pulezidenti yemwe aamamusankha.

Apa nkhani inali yoti kodi ndi koyenera kuti Pulezidenti adzisankhidwa limodzi ndi wachiwiri wake. Maganizo atatu anatuluka mumutuwu.

Maganizo oyamba anaona kuti zinthu zikhale momwe ziliri panomu. Omwe anawona kuti zinthu zikhale chocnhi anati ntchito za wachiwiri wa Pulezidenti ndi zosiyana ndi za Pulezidenti choncho anayenera kulandira mphamvu kuchokera ku anthu mogwirizana ndi ndime 12 ya malamulo a dziko lino. Iwo anati oyamba wachiwiri kwa Pulezidenti amapatsidwa mphamvu kugwirizira udindo wa u Pulezidenti ngati Pulezidentiyo atadwalika kwambiri. Kotero ndi kosafunika kuti munthu yemwe sanasankhidwe pa mpando wa wachiwiri wa Pulezidenti kugwira ntchito za Pulezidenti yemwe anthu anampatsa mphamvu zolamulirapodzera pa chisankho. Izi zidzathandiza kupereka mphamvu za ulamuliro.

Gululi linapempha kuti pa zokambirana pa mutuwu, anthu asakakamizidwe mmaganizo potengera mmene ziliri ndale

pakali pano koma akaganize mofatsa ndi mozama pankhani yokhudza malamulo ndi ntchito za ulamuliro. Iwo anati kuthana ndi mavuto ngati amenewa, ndi pofunika kuti ziapni za ndale zisamakakamize owayimira ndi wachiwiri wake koma adzisiyira ntchito achiwiri wa Pulezidenti monga imanenera ndime 80 (3) ya malamulo yomwe imafunsa oyimira u Pulezidenti kutchula munthu amene adzakhale wachiwiri wake.

Maganizo achiwiri ndi ofuna kuti njira yosankhira wachiwiri wa Pulezidenti isinthike. Apa akuti Pulezidenti akangosankhidwa pa mpando apatsidwe mphamve zosankha wachiwiri wake. Izi zingachepetse mavuto omwe angagwe ngati awiriwa angalephere kumvana pa zinthu zina kapena kuti sakuonana diso ndi diso. Zinakambidwanso kuti ndipofunika kuyika dongosolo kuti nduna ndi wachiwiri wa Pulezidenti adziyang'anira ntchito za boma podikira chisankho pofuna kuthana ndi dandaulo loti munthu amane sanasankhidwe adzilamulira dziko lino.
Maganizo achitatu anali oti amene akhale wa chiwiri pa chisankho ndiye adzikhala wachiwiri wa Pulezidenti. Apa panamveka kuti pali chitsimikizo ali ndi anthu ambiri omutsatira choncho akhonza kukhala ndi mphamvu za ulamuliro.

## 5.4 Ofesi ya Wachiwiri kwa Wachiwiri kwa Pulezidenti

Ndime 80 (5) ya malamulo imapereka mphamvu kwa Pulezidenti kusankha munthu pa udindo wa Wachiwiri kwa Wachiwiri wa Pulezidenti pamene ataona kuti ndi kotero komanso mokomera zofuna za aMalawi. Gawo limeneli linayikidwa ndi nyumba ya malamulo kudzera Act No. 6 ya 1995 ndipo cholinga chake chinali choti chipani chinali kulamulira panthawiyo United Democratic Front (UDF) chipeze mphamvu zambiri mnyumbayi pogwirira ntchito limodzi ndi chipani cha Alliance for Democracy (Aford). Chifukwa china chinali chofuna kuti mu boma mukhale oyimirira kuchokera muzigawo zonse za dziko lino. Ndipo amene anakhalapo pa udindo umenewu kawiri konse ndi a Chakufwa Thom Chihana, Pulezidenti wa Aford.

Mumisonkhano yonse anthu anaona kuti ndi kosafunika kuti mpandowu upitilire kukhalapo. Anati mpandowu ulibe ntchito yake yeniyeni kotero ndi osafunikira. Chifukwa china, anthu akuopa kuti Pulezidenti akhonza kumagwiritsa ntchito molakwika posankha munthu okhala paudindowu. China nthumwi zinaona kuti Malawi ndi dziko laling'ono komanso chiwerengero cha anthu ndi chosafunika anthu atatu kukhala pa maudindo apamwambawa. Powonjezera nthumwi zinaonanso kuti Malawi ndi dziko losauka ndipo kukhala ndi anthu atatu pa maudindo apamwambawa ndi kusaganizira anthu ochuluka osauka omwe amakhala kumidzi. Apa anati ndimeyi inabwera

chifukwa cha ndale zofuna kusangalatsa anthu ena ndima odzikonda.

Nthumwi zina zinaona kuti zinthu panopa ndi zolimbikitsa kugawikana mmzigawo ndi ndale zokuti Pulezidenti ayenera kumachokera kuchigawo chakummwera, wachiwiri oyamba chigawo chapakati ndipo wachiwiri kwa wachiwiri adzichokera kuchigawo chakumpoto popeza ndiko kuli anthu ochepa.

## 5.5 Kuchuluka Kwa Nduna

Ndime 92 (1) ya malamulo linakhazikitsa bungwe la Nduna za Boma lomwe nthumwi zake ndi Pulezidenti, wachiwiri wake oyamba, wachiwiri wake wachiwiri, nduna ndi achiwiri kwa nduna onse, omwe angasankhidwe ndi Pulezidenti pa nthawiyo. Bungwe la ndunali linapatsidwa mphamvu ndi kugwira ntchito monga mmene bukhu lamalamulo kapena malamulo a nyumba ya malamulo ikunenera polangiza Pulezidenti molingana ndi mfundo zoyendetsera boma kapena tchito zina zomwe Pulezidenti angawapemphe kutero.

Ndime 94 (1) imapatsa mphamve Pulezidenti kusankha nduna kapena achiwiri kwa nduna ndi kusankhira munthu wina ngati ngati mpando wina mubungwe la ndunali palibe munthu. Pulezidentiyu anapatsidwa mphamvu zonse kuona ndi kuganizira kukula kwa bungwe la ndunali.

Tisanafike mchaka cha 1994 kuchuluka kwa nduna kunali khumi ndi zinayi (14). Koma titadutsa 1994 chiwerengero cha nduna chinafika pa 47. Panopa chiwerengerochi chili pa 30 kuphatikiza nduna ndi achiwiri awo.

Nthumwi ku zokambiranazi zinaunika kuti kuchuluka kwa nduna kuziganizira mavuto a zachuma omwe ali mdziko muno. Zaoneka kuti boma lomwe linali mmbuyomu silimalabadira za mavuto amenewa, kotero ndi kwabwino kuti kachulukidwe ka nduna kadziongoleredwa ndi malamulo a dziko lino. Koma nthumwi zinalephera kumvana pa chiwerengero chomwe chidzikhala chovomerezeka. Ena amaganiza kuti 14, ena 15 pamene ena amati chiwerengerochi chidzikhala makumi awiri (20) kuphatikizapo ndi nduna zomwe. Nthumwi zinaonanso kuti ndi kwabwino kuti nduna adziphatikiza maudindo ngati mmene zinthu zinaliri mmbuyo mwa chaka cha 1994. Nthumwizi zinaonanso kuti maudindo a anduwa adzilembedwa mu bukhu la malamulo ngati mmene ziliri kumaiko ena monga Switzerland. Kuonjezera kwa udindo kulikonse kudzivomerezedwa ndi nyumba ya malamulo.

Mafumu a chigawo cha kumpoto anati sakuona kufunika kwa maudindo a wachiwiri kwa nduna, chifukwa ntchito zomwe

achiwiri kwa nduna angagwire zikhoza kugwiridwa ndi alembi a m'maunduna. Apa pndiye kuti maudindo a wachiwiri kwa nduna ayenera kuthetsedwa.

## 5.6 Nkhani Zina

### 5.6.1 Nthawi Yokhala pa Udindo Pulezidenti ndi Wachiwiri Wake

Ndime 80 (3) ikufotokoza kuti Pulezidenti ndi achiwiri ake akhonza kukhala pa maudindo awo kosaitirira maulendo awiri motsogozana.

Mabungwe omwe si aboma amanenetsa kuti kalembedwe ka ndime 83 (3) kaunikidwenso kuti Pulezidenti opuma asamayimirenso ndale akachoka pa mpandowu atagwira ntchito yake. A chipani cha Malawi Congress nawo anayikirapo ndemanga kwambiri pa mfundo imeneyi.

Nthumwizi zinamvana za kuchotsa Pulezidenti kapena wachiwiri wake pa udindo. Mfundoyi ikufotokozanso kuti payenera kukhala ndondomeko zochotsera pa udindo wa Pulezidenti ndi wachiwiri wake potsatira malamulo oyendetsera nyumba ya malamulo pokhapokha patakhala zoyenereza kutero potsatira chilungamo cha chibadwidwe. Pulezidenti kapena wachiwiri wake angachotsedw pa maudindo awo ngati aphwanya malamulo oyendetsera dziko la Malawi.

Nthumwi zinaonetsa kusakhutira ndi kufotokoza kumeneku chifukwa kugwiritsa ntchito malamulo oyendetsera nyumba ya malamulo pankhani yofunika ndipo yayikulu chonchi sikunali koyenera. Apa mabungwe omwe siaboma anaganiza kuti mfundo zimenezi ziyenera kuti ziphatikizidwe mumalamulo oyendetsera dziko lino. China ndi chakuti ndondomeko imeneyi iyenera kukhazikitswidwa ndi nyumba ya Seneti yomwe ndi nyumba ya pamwamba ya malamulo.

Apa panaganiziridwanso kuti mfundo zochotsera Pulezidenti kapena wachiwiri wake zidzigwiritsidwa ntchito pokhapokha patachitika chisankho chomva maganizo a anthu pankhaniyi powonetsa kuti anthu agwirizana nazo. Izi zingathandize kuletsa kugwiritsa molakwika mphamvu yochotsa Pulezidenti ndi wachiwiri wake paudindo.

### 5.6.2 Ndondomeko zochochotsera Pulezidenti Kapena Wachiwiri Wake pampando

Ndime 86 (1) imafotokoza kuti munthu wokhala pa udindo wa Pulezidenti kapena Wachiwiri wake angachotsedwe paudindo ngati atapezeka olakwa potsata njira yovomerezeka. Ndime yaing'ono (2) imafotokoza kuti ndondomeko yoyenera kutsata iyenera kukonzedwa potsatira malamulo oyendetsera nyumba ya malamulo.

Zambiri zinakambidwa pa mfundo imeneyi ngakhale nthumwi sizinagwirizane kalikonse. Koma kunali kufunsa mafunso monga : kodi Pulezidenti kapena wachiwiri wake omwe amuchotsa pampando adzichita naye chiani? Kodi ndi woyenera kuti adzilandira zinthu zomwe Pulezidenti wopuma ayenera kulandira? Poganizira ndime 91 yomwe imafotokoza kuti Pulezidenti yekha sayenera kuzengedwa mulandu, nanga wachiwiri wake nkhaniyi ikuti bwanji. Kodi mbiri ya umbanda ikhonza kukhala njira imodzi yomuchotsera pa mpando, kodi wachiwiri kwa Pulezidentiyo ayenera kumazengedwa mulandu?

### 5.6.4 Kusintha Zipani kwa Pulezidenti

Ndime 80 (1) ya malamulo imafotokoza kuti Pulezidenti ayenera kusankhidwa pa udindo potsatira malamulo ndi mmene lamulo lokhazikitsidwa ndi a phungu a ku nyumba ya malamulo linganenere. Ndime 32 (3) yokhudza chisankho cha aphungu ndi Pulezidenti imaunika mmene munthu akhoza kusankhidwa ngati Pulezidenti. Ndimeyi imafotokoza kuti munthu akhoza kupikisana poyimirira chipani kapena munthu kupikisana poyima payekha.

Maganizo ambiri anaperekedwa makamaka pa nkhani ya Pulezidenti osiya chipani chake ali pa udindo. Maganizo oyamba anali okuti Pulezidenti ali ndi ufulu ndipo ayenera kuchita zinthu zomwe akuona kuti ndi zokomera dziko. Kunaonedwa kuti ngati ngati angakakamizidwe kutsatira mfundo za chipani, ntchito yoyendetsera dziko ikhoza kusokonezeka.

Mfundo yachiwiri ndi yakuti Pulezidenti adzikhudzidwanso ndi ndime 65 ya malamulo ngati aphungu popeza onse ndi ochita kusankhidwa pa maudindo awo. Apa panaoneka kuti ndikoyenera kukhazikitsa lamulo loletsa pulezidenti kusintha zipani. Chifukwa chakuti ndime 32 (3) ya malamulo pa za chisankho cha aphungu ndi Pulezidenti amati munthu akhoza kulamulira dziko ngati atasankhidwa ali oyima payekha kapena ngati ali oyimira

chipani cha ndale. Apa zidzathandiza kuti munthu asamaganize zodziwa yekha akatero ndiye kuti ayitanitse chisankho kuti anthu amusankhenso ngati ndi kotero. Komabe nthumwizi zinaona kuti pakhoza kukhala zinthu zina zomwe zingamupangitse Pulezidenti kuchoka mu chipani chake ndipo zikatero ayenera kuloledwa kulamulira ngati oyima payekha.

Mfundo yachitatu inali yofuna kuthana ndi vuto loyika chidwi pa ndale za chipani mmalo moganizira zokweza ntchito za chitukuko cha dziko. Mmaganizo awo anthuwa anaona kuti ndi bwino kuti Pulezidenti akangosankhidwa pampando kudzera mchipani adzitula pansi udindo wake wandale kuti adzitha kuona ntchito zokweza dziko ndi chidwi. Koma vuto lake likhoza kukhala pa chisankho chotsatira zomwe sizinaunikidwe.

### 5.6.5 Kusintha Udindo wa Pulezidenti

Pa misonkhano yomwe inachitika ku chigawo cha kumpoto, nthumwi zinaona kuti udindo wa Pulezidenti udzikhala osinthana poyendera zigawo zitatu zomwe zili mdziko muno. Zinaoneka kuti kumpoto chiwerengero cha anthu ndi chochepa ndipo ndi mmene ndale ziliri ndi kovuta kuti Pulezidenti angasankhidwe kuchokera ku chigawocho. Iwo anachiwona kuti chikhoza kukhala cha mwayi chuma, chitukuko zizitha kugawika mofanana kuposa pakali pano.

## MUTU 6

## 6. NTHAMBI YA BOMA YOLAMULA

### 6.1 Msinkhu wopumira pantchito majaji

Ndime 119 (1) (b) ikunena kuti munthu yemwe ndi Jaji adzapuma pa ntchito yake ya ujaji akwanitsa zaka makumi asanu ndi limodzi kudza mphambu zisanu zakubadwa. Ndipo ndime 113 (3) ya malamulo a dziko lino ikunena kuti Mamajesitileti ndi anthu ena ogwira ntchito ku Bungwe loona za malamulo adzipuma pa ntchito akakwanitsa zaka makumi asanu ndi ndi awiri zakubadwa.

Pokambiriana ndi akatswiri a zamalamulo, anthu ambiri anali ndi ganizo loti ndi bwino kuti ma Jaji nawonso adzipuma pa ntchito akakwanitsa zaka makumi asanu ndi awiri zakubadwa. Anthuwo anati ndi sosamveka kuti ma Jaji adzipuma pa ntchito mofulumira kusiyana ndi ma ofesila ena oona za malamulo omwe ali ang'ono pa undindo. Iwo anati kuonjezera zaka zopuma pa ntchito za ma Jaji kufika pa makumi asanu ndi awiri za kubadwa, kudzapereka ulemu kwa ma Jaji komanso zidzanthandiza kuti ma Jaji opuma asakhale ndi maganizo ofuna kupeza ntchito kwina.

Ndipo mulipoti lake pa nkhaniyi, Bungwe Lounikanso za Malamulo a dziko lino la Malawi Law Commission, linati zaka makumi asanu ndi awiri ndi zomwe ma Jaji a mapumila pa ntchito mu dera lino la Africa Koma bungweli likuti ndi bwino kuti kukweza kwa zakazi kuvomelezedwe ndi a phungu a nyumba ya malamulo.

Komabe, panali anthu ena ochepa omwe anali ndi maganizo oti nkosafunika kuti zakazi zionjezeredwe. Nawonso ma bungwe omwe siaboma anati nkosafunika kutero chifukwa magwiridwe a ntchito amunthu amakhala ochepa munthuyo akamakula mu zaka zakubadwa. Kusasintha kwa zakaku kudzathandiza kuti a chinyamata a khale ndi mwai otenga mau undindo ofunika akanali a chichepere. Choncho, chifukwa chaichi, ndi bwino kuti zaka zopumila pa ntchito za ma Majisitileti zisinthidwe kuchoka pa zaka makumi asanu ndi awiri kufika pa zaka makumi asanu ndi limodzi kudza mphambu sisanu monga momwe ziziri ndi ma Majaji.

### 6.2 Msinkhu woyenera kuti munthu atha kusankhidwa kukhala jaji

Ndime 112 ikunena kuti munthu akhoza kusakhwidwa kukhala Jaji munjira ziwiri. Njira yoyamba: ngati munthuyo ali Jaji kapena ngati anakhala Jaji wa khothi lozenge milandu ikukuikulu kapena ing'ono ing'ono. Njira ya chiwiri: ngati munthu ali oyenera kugwira ntchito ya za malamulo, kapena kulimbikitsa za malamulo, kapena kukona za malamulo ndipo kuti wa gwira ntchito yotereyi kwa zaka zosachepera khumi.

Malamulo a dziko lino sakunena zaka zomwe munthu zingamuyenereze kuti asakhwidwe Jaji. Pa nsokhano wa akatswiri a za malamulo, panatuluka

maganizo awiri pa nkhaniyi. Ganizo loyamba linali loti, zaka zomwe munthu angasakhwodwire Jaji zilembewdwe m'malamulo a dziko lino ndipo kuti zakazo zikhale makumi anayi. Izi zidzanthandiza kuti munthu yemwe angasakhwidwe kukhala Jaji adzikhala wodziwa bwino ntchito yake, wa luntha ndi wokhwima maganizo. Akatswiriwa anati kale munthu samasakhwidwa kukhala Jaji ngati zaka zake za kubadwa zinali zosakwana makumi anayi.

Ganizo lachiwri linali logwirizana ndi kuzisiya zinthu monga momwe ziriri pano. Ganizoli likuti kuyika zaka zomwe munthu ayenera kusakhwidwira Jaji sikungathandize kuti Munthu akhale wa nzeru kapena wodziwa bwino ntchito.

### 6.3 Wachiwiri kwa Wamkulu wa majaji

M'malamulo a dziko lino mulibe zokhazikitsa ofesi ya wa chiwiri kwa mkulu wa Majaji. Koma m'maiko ena, monga dziko la South Africa, malamulo akulola kukhala ndi ofesi ya wachiwiri kwa mkulu wa ma Jaji.

Pokambirana nkhaniyi, anthu anati ndi kofunika kuti malamulo a dziko linonso adzilola kukhazikitsa ofesi ya wa chiwiri kwa mkulu wa ma Jaji.

Ofesi ya wachiwiri kwa mkulu wa ma Jajiyu idzankhala ngati momwe iliri ofesi ya wa chiwiri kwa Nduna ya Boma kapena Sipikala wa nyumba ya Malamulo. Izi zidzathandiza kuti ntchito ya mkulu wa Majaji idziyenda bwino ngakhale iye palibe.

### 6.4 Ofesi yoona za malamulo

Ndime 111 (4) ikutanthauzila ofesi ya zamalamulo kuti ndiyo ofesi ya mkulu woona za malamulo,wogwirizila wake, kapena Jaji wa khoti lalikulu la High khoti kapena wogwirira wake, mkulu wa khoti lalikulu la Supulimu kapena wachiwiri wake, majisitileti kapena munthu yemwe amazenga milandu ku makhoti a mafumu kapenamakhoti ena.

Tanthauzo ili silikuphatikiza wa pampando kapena wachiwiri kwa wapampando wa khoti loona nkhani za anthu a pa ntchito, lomwe liri khoti lokhazikitsidwa ndi ndime 110 (2) ya malamulo a dziko lino. Iyi ndi mbali imodzi yoyiwalika yomwe iyenera kukonzedwa. Choncho nthumwi za kumsonkhano mokambirana zankhaniyi zinati nkofunika kuti ofesi ya wa pampando wa khoti lomva madandaulo a anthu a pa ntchito pamodzi ndi ofesi ya wachiwiri wake, itanthaizidwanso m'malamulo a dziko lino.

### 6.5 Bungwe loona za ogwira ntchito za khothi

Ndime 117 ikufotokoza za anthu oyenera kukhala mu komishoni yoona za bungwe la za malamulo. Anthu okhala mu komishoni imeneyi ndi awa : wamkulu wa ma jaji monga wapampando, wapampando wa komishoni ya anthu ogwira ntchito m'boma la Civil Service Komishoni, kapena womayimirira wake, mkulu wa

khoti la apilu kapena jaji, munthu wa zamalamulo ndi majisitileti monga angasankhidwire ndi Pulezidenti mogwirizana ndi mkulu wa majaji. Mamembala ndi maofesisala atatu a za malamulo, munthu m'modzi wodziwa za malamulo ndi munthu m'modzi ogwira ntchito za boma.

Pa msonkhano wa ma ofesala a zamalamulo, panali kusakhutira ndi anthu a mu komishoni chifukwa ambiri mwa anthuwa ndi a za malamulo. Choncho, msonkhano udamanga mfundo yoti anthu enanso oyenera omwe si a zamalamulo asikhala nawo mukomishoniyi.

Bungwe la Malawi Law Komishoni lalandira pempho (submission) kuchokera ku komishoni yoona za malamulo loti pakhazikitsidwe malamulo opatsa mphamvu komishoniyi kukhala yoyima payokha. Bungwe la Malawi Law Komishoni likuganizira pempholi.

## 6.6 Kusankha majaji

Malamulo adziko lino, kupyolera mu ndime 111 (2) akunena kuti ma Jaji adzasankhidwa ndi Pulezidenti potsatira chiyamikilo cha komishoni yoona za malamulo.

Maofesala woona za malamulo anaona kuti izi sizitsatiridwa. Nthawi zambiri ma Jaji amasankhidwa popanda chiyamikilo cha komishoni yoona za malamulo. Ndikoyenera kuti ndime 111 (2) idzitsatidwa posankhama Jaji.

## 6.7 Kuchotsa majaji pampando

Ndime 119 (3) ikupereka mphamvu kwa Pulezidenti, mogwirizana ndi komishoni yoona za malamulo, yochotsa Jaji. Mphamvu zimenezi zingagwiritsidwe ntchito aphungu a nyumba ya malamulo atakambirana ndi kugwirizana kuti nkoyenera kuti Jaji achotsedwe. Zifukwa zomuchotsera Jaji ndi kulephera kugwira ntchito komanso khalidwe loipa lomwe Jaji angaonetse. Ndimeyi ikuti ndondomeko zochotsera Jaji ziyenera kugwirizana ndi mfundo za chilungamo cha chibadwidwe.

Maofesala a za malamulo ataunika ndimeyi anaona kuti siyikufotokoza bwino ndondomeko zochotsera Jaji mogwirizana ndi mfundo za chilungamo chachibadwidwe. Nkoyenera kuti ndimeyi ilembedwenso bwino.

## 6.8 Khothi lomva madandaulo a anthu ogwira ntchito

Khoti loona za madandaulo a anthu a pantchito linakhazikitsidwa ndi ndime 110 (2) ya m'malamulo a dziko lino kukhala khoti loyang'aniridwa ndi khoti lalikulu la High Khoti. Pa

msonkhano wake ndi maofesala woona za malamulo, khotili linapempha kuti lileke kukhala pansi pa bungwe la za malamulo ndikuti m'malo mwake likhale (Tribunal). Izi zidzathandiza kuti milandu ya apilu idzipita ku khoti la apilu lalikulu la supulimu.

Ganizo lina pankhaniyi linali loti khotili likhale lapadera ndi mkhala pa mpando awke-wake ndi wachiwiri wa mkhala pa mpando.

## 6.9 Khothi lounika malamulo

M'malamulo a dziko lino muli ma khoti akuluakulu awiri. Makhotiwa ndi awa : Khoti la apilu la Supulimu ndi khoti la High Khoti. M'malamulowa analetsa kukhazikitsa makhoti ena oposela awiriwa kapena ofanan nawo.

Komabe nyumba ya malamulo inakhazikitsa khoti lina lapadera loona za malamulo a dziko lino. Khotili limagwira ntchito pakakhala pofunika. Malingana ndi maofesala a za malamulo, khotili likugwira bwino ntchito yake. Komabe pakufunika kulimbikitsa ntchito za khotili kuti likhale lokhazikika. Ngakhale kuli kofunika kulimbikitsa ntchito za khotili, maofesala a za malamulo akuti kudzakhala kovuta kutero chifukwa cha ndime 103 (3) ya malamulo a dziko lino yomwe ikuletsa kukhazikitsa ma khoti oposa kapena ofanana ndi khoti lalikulu la apilu la Supulimu kapena la High khoti.

## 6.10 ZINA NDI ZINA

### 6.10.1Malipiro a Wamkulu wa majaji

Pounika za malipiro a mkulu wa ma Jaji, ma ofesala a za malamulo anaona kuti malipirowo ndi osakwanira. Ganizo linaperekedwa kuti malipiro a mkulu wa ma Jaji adzifanana ndi a wachiwiri kwa Pulezidenti wa dziko.

### 6.10.2 Ndalama Zoyenedtsera ntchito za makhothi

Maofesala a za malamulo anafotokoza za mavuto omwe ofesi ya za malamulo limakumana nalo chifukwa cha kuchepa kwa ndalama zoyendetsera ntchito zake zomwe imalandira kuchokera ku boma. Iwo anapereka njira ziwiri zomwe zingathandize kuthetsa vutoli. Njira yoyamba ndi yosankha ofesala wa za malamulo kukhala membala wa bungwe la nduna za boma.

Njira yachiwiri, ndikuonetsetsa kuti ndime 183 ya malamulo ikutsatidwa. Izi zidzathandiza kuti ofesi ya za malamulo ikupatsidwa ndalama zokwanira zogwirira ntchito zake.

**MUTU 7**

## 7. MABUNGWE OKHAZIKITSIDWA NDI MALAMULO OYENDETSERA DZIKO LINO

### 7.1 Bungwe Loona za Ufulu Wachibadwidwe wa Anthu

Ndime 129 ya malamulo ikukhazikitsa bungwe loona za ufulu wachibadwidwe wa anthu ndi cholinga chofuna kuteteza ufulu wao wachibadwidwe kunkhanza zomwe angachitiridwe kapena ku zinthu zomwe zingawaphwanyire ufulu wao.

Mubungweli muli mkulu wa za malamulo, mkulu womva madandaulo a anthu ndi anthu ena ochokera m'mabungwe ena odziwika. Anthuwa amasankhidwa ndi mkulu wa za malamulo mogwirizana ndi mkulu womva madandaulo a anthu.

Pali kusakhutira ndi masankhidwe a makomishonala a bungweli kupatsa mphamvu yosankha makomishonala kwa mkulu wa za malamulo ndi mkulu womva madandaulo a anthu kukuonetsa bungwe loona za ufulu wa anthu wachibadwidwe kukhala ngati kuti liri pansi pa ma ofesi akuluakulu awiriwa pamene siziri choncho. Choncho nkofunika kuti kasankhidwe ka makomishonala a bungweli kaunikidwenso. Nkofunikanso kuti bungwe lipatsidwe mphamvu loima pa lokha.

Komanso nthcito za bungweli zikufunikanso kuziunika bwino. Ndime 129 ndi 130 za m'malamulo a dziko zikunena kuti ntchito za bungweli ndi kuteteza ufulu wachibadwidwe komanso kufufuza izo zomwe zingaphwanye ufuluwu. Ntchito izi ndi zomwenso mabungwe ena woona za ufulu wachibadwidwe akugwira. Pa chifukwa ichi, nkofunika kuti ndime 129 ya malamulo ikonzedwenso chimodzimodzinso ndime (30) 130

### 7.2 Ofesi ya Mkulu Womva Madandaulo a Anthu

Ofesi ya nkulu womva madandaulo a anthu ikukhazikitsidwa ndi ndime 120 ya malamulo. Ntchito ya ofesiyi ndi kufufuza milandu yomwe ikusowa chilungamo chifukwa choti siyinapite ku khoti. Ndime 5 ya malamulo lomwe likukhazikitsa ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu, siyikupereka mphamvu ku ofesi ya mkuluyu yofufuza milandu yomwe ikukhudza anthu ogwira ntchito m'boma ndi m'makampani a boma. Pa chifukwa ichi, nkofunika kufotokoza momveka bwino ntchito ya ofesi ya mkulu womva madandaulo a anthu.

## MUTU 8

## 8. ZIGAWO ZINA ZA BOMA

### 8.1 Komiti ya za Chitetezo

Iyi ndi komiti ya kunyumba ya malamulo ndipo imakhazikitsidwa kudzera pa ndime 162 ya malamulo. Anthu amukomitiyi amasankhidwa molingana ndi mipando ya aphungu yomwe ali nayo mnyumbayi ndipo ayenera kukhala pa maudindo awo kwa chaka chimodzi. Ntchito ndi mphamvu ya komitiyi zimaperekedwa molingana ndi malamulo a dziko lino komanso malamulo oyendetsera nyumba ya malamulo.

Zinaoneka kuti ntchito za komitiyi ndi zosamveka bwino ndipo ndikofunika kuzilongosola bwino.
Kachiwiri nthumwi zinaona kuti nthawi yokhala mu komitiyi ya chaka chimodzi ndi yosayenera koma adzikhala zaka zisanu (5) mogwirizana ndi nthawi yokhalira pa udindo wa uphungu.

Oyimira a gulu lachitetezo kumisonkhano ya komitiyi adadzetsanso nkhawa pakufunika kwa ndime 161 (3) powonjezera mphamvu za ulangizi posankha maudindo a chitetezo malingana ndi ndime yaying'ono 2 (b) ya ndime 161.

### 8.2 Dipatiment yoona za Anthu Olowa ndi Kutuluka m'dziko muno

Ili ndi gawo limodzi la unduna wa za mdziko ndi za a police. Koma mmbuyomu inali mbali imodzi ya a police choncho linalinso gulu limodzi la chitetezo.

Padakali pano zikuoneka kuti sizikudziwika kuti kodi adakali mbali ya chitetezo kapena bungwe la anthu wamba. Poganizira kufunikira kwa bungweli pankhani za chitetezo ndi kofunika kuliyika pa mutu wakewake mu malamulo a dziko lino ndi kulongosola bwino ntchito zake. Mutuwu ndiofunanso kuti ulongosole ndi kulimbikitsa bungweli kugwira ntchito modziyimira pawokha komanso mwa ukadaulo.

### 8.3 Bungwe Lolimbana ndi mchitidwe wa Ziphuphu

Bungweli analikhazikitsa kudzera pa malamulo okhudzana ndi ziphuphu ndipo cholinga chake ndi kuthana ndi ziphuphu mboma komanso mmabungwe ena onse omwe siaboma komanso a anthu wamba.

Nthumwi zinasindikizanso kufunika kokweza bungweli kuti likhale mbali imodzi ya malamulo a dziko lino poyang'anira ntchito yomwe bungweli likugwira polimbana ndi ziphuphu

mdziko muno. Popereka maganizo amenewa nthumwi zinaonanso mozama mfundo zomwe zikupezeka pa ndime 13 (0) zimene zimafunsa boma kukhazikitsa njira zolimbikitsa kupanga zinthu mosabisa, kusamala chuma polimbikitsa chikhulupiriro ndi ulamuliro wabwino.

## 8.4 Banki Lalikulu la Boma

Ndime 185 inakhazikitsa banki ya lizevu ngati bank yayikulu ya mdziko muno. Bankili limathandiza kuongolera kayendetsedwe ka ndalama ndi mabungwe onse oyendetsa za chuma.

Apa nthumwi zapempha kuti nkofunika kulimbikitsa bungweli kuti likhale loyima palokha podzera mumalamulo a dziko lino. Komanso mfundo zokhazikitsira ma Banki ziyenera kukhala zotetezedwa kuopetsa zomwe zinachitika mbuyomu pomwe nyumba ya seneti inathetsedwa mwachisawawa popeze onsewo ndi mabungwe a dziko lino.

## 8.5 Bungwe Loona za Ogwira Ntchito Mmboma

Padakali pano, pndime 186 ya malamulo padakhazikitsidwa bungwe loona za ogwira ntchito mmboma ndipo bungweli linapatsidwa ntchito yoyendetsa komanso kutsimikizira za anthu omwe alembedwa ntchito mmboma. Padakali pano palibe bungwe loti lidziona mabungwe atsopano ngati loona za malamulo (Law Commission), lothana ndi ziphuphu komanso lowona za chisankho omwe adadza patadutsa chaka cha 1994.

Pakukambirana kunaonedwa kuti ndikofunika kukhazikitsa bungwe lalikulu lomwe lidzigwira ntchito za bungwe lowona za ogwira ntchito mmboma lomwe lidzitchedwa Public Service Commission kuti lidziyang'anira mabungwe ena onse. Mabungwe ena onse kuphatikizapo loyang'anira ogwira ntchito mmboma (Civil Service Commission) adzakhala pansi pa bungwe lalikulu ndipo oyenera kudzapatsidwa ntchito zawo kudzera ku malamulo a anthu ogwira ntchito za boma.

Kachiwiri zinaonedwanso kuti bungwe lalikululi ndilofuna kulipatsa mphamvu zoti lithe kukhala loyima palokha pothandiza kuti lidzigwira ntchito zake bwino popanda olisokoneza.

## 8.6 Apolisi

Ndime 154 ya malamulo inakhazikitsa Ofesi ya Inspector General of Police ngati wamkulu wa asilikali a chitetezo cha mdziko (Polisi). Mkuluyi amasankhidwa ndi Pulezidenti koma amafunika kuti akatsimikizire a kunyumba ya malamulo pochita voti.

Pakukambirana paoneka kuti sikofunika kuti a kunyumba ya malamulo azikatsimikizira kusankhidwa kwa mkulu wa polisi. Izi zili chomwechi chifukwa chakuti kusankhidwa kwa mkulu wa asilikali a Malawi Defence Force sayenera kuvomerezedwa ndi nyumba ya malamulo. Choncho ndi kofuinika kuti pasakhale kusiyana pa mbali ziwirizi.

## 8.7 Bungwe la mafumu

Mumalamulo a dziko lino a mchaka cha 1966, umba wa mafumu unali ovomerezeka kudzera pa ndime 6 ndipo unafotokoza kuti: “Umba wa mafumu uyenera kuvomerezeka ndi kutetezedwa mdziko muno, pothandiza kuti mafumu athe kuthandiza pa ntchito zokweza dziko podzera mu maufumu wawo.”

Kufotokezera kumeneku kukupezeka pa MUTI 1 omwe unali mumalamulo a dziko lino. Kafukufuku yemwe anapanga a bungwe lowona za malamulo likusonyeza kuti mayiko ambiri omwe analandira ufulu odzilamulira anaphatikiza mumalamulo a mayikowo ntchito za mafumu. Ku maiko ngati Tanzania komwe maufumu anathetsedwa, anachotsa gawo limeneli mumalamulo.

Ku Malawi kuno ngakhale malamulo safotokoza momveka kufunika kwa mafumu, komabe amapatsidwa mpata otenga nawo mbali pa ntchito za chitukuko cha dziko. Kudzera pa ndime 68 yas malamulo ndi ndime yaying’ono (1) (b) mfumu imodzi kuchokera boma lili lonswe inapatsidwa mpata okhala mu seneti.

Chimodzimodzi, ndime 146 (4) imayenereza nyumba ya malamulo kuonetsetsa kuti “mukomitiyi ya mabowa ang’ono muyenera kukhala chiwerengero chovomerezeka cha mafumu mmadera.”

Apa panaonedwa kuti sichinali cholinga kuti ntchito ya mafumu ithetsedwe. Pokambirana ndi mafumu mdziko lonse lino iwo anafotokoza kuti ndi koyenera kusintha malamulo kuti ntchito yawo idzikhala yozindikiridwa monga mmene zinaliri m’mbuyomu tisanafike mchaka cha 1994. Mabungwe omwe siaboma, a chipembedzo, andale, komanso akulu akulu a za maphunziro mchigawo chakumpoto akugwirizananso ndi maganizowa.

## MUTU 9

## 9. ZINA NDI ZINA

### 9.1 Kuvomereza ndi kusainira malamulo okhudza maiko a padziko lapansi

Ndime 89 (1) (f) imapatsa mphamvu Pulezidenti kukambirana, kugwirizana kapena kupatsa mphamvu nduna ndi akazembe.

Pazokambirana ndi bungwe la amayi omwe ndi aphungu a kunyumba ya malamulo, kunaonedwa kuti ndi kwabwino kuti mphamvu zimenezi azipereke ku nyumba ya malamulo, pogwirizana ndi m'mene zinthu ziliri m'maiko ena onse. Kunaonedwanso kuti maganizo opereka udindo kwa munthu kugwira ntchito ku maiko kapena mabungwe akunja kukhale m'manja mwa nyumba ya malamulo.

### 9.2 Mkulu wolangiza Boma pa za malamulo

Ndime 98 (1) ya malamulo inakhazikitsa ofesi ya mlangizi wa za malamulo ngati mlangizi wamkulu wa boma pa nkhani za milandu. Ndime yaying'ono (2) ya ndime 98 imanena kuti ofesi ya mlangiziyi ikhoza kukhala ya nduna kapena ya munthu ogwira ntchito za boma.

Apa nthumwi zinaonetsa kusakhutitsidwa ndi mmene anthu akhala pa udindowu amagwirira ntchito zawo chivomerezereni malamulo amene alipowa mchaka cha 1994. Apa anthu anaona kuti ndi udindo umenewu usamakhale wa nduna kuti udzitha kugwira ntchito yake mosakondera komanso kuti udzitha kutumikuira mbali zonse sitatu za boma. Apa nthumwi zinanenetsa kuti udindo umenewu ukhala wa munthu ogwira ntchito za boma poopetsa kulowetsa ndale pa udindowu.

### 9.3 Kuulula chomwe potenga mpando wosankhidwa

Ndime 88A(1) ya malamulo imapempha Pulezidenti ndi ndi nduna kuulula katundu ndi mabizinesi omwe ali nawo pasanathe miyezi itatu chiasankhire pamipando yawo.

Ndime 213 inaphatikiziranso aphungu akunyumba ya malamulo, akulu akulu ogwira ntchito za boma komanso mabungwe omwe ndi aboma. Malamulowa akupatsanso mphamvu nyumba ya malamulo kuona maudindo ena omwe angafunike kuti adziuulula kuchuluka kwa katundu wawo. Pakali pano nyumbayi sinachitepo izi.

Kuchuluka kwa katunduyu ndi mabizinesiwa kuyenera kuchitika polemba chikalata ndi kukachipereka kwa Sipikala wa Nyumba ya Malamulo amene ayenera kuchipereka ku ofesi yoyenerezedwa malingana ndi malamulo oyendetsera nyumba ya malamulo.

Pazokambirana nthumwi zinaona kuti lamuloli likusowa mphamvu chifukwa chosowa zoliyenereza kutero. Apa kudaonedwa kuti andale onse adziulula katundu wao yense amene ali naye asanawalumbiritse pa maudindo awo. Izi zidzachepetsa kukula mtima ndi mwano.

Kachiwiri kunaoneka kuti kuulula katundu kwa Sipikala wa nyumba ya malamulo nkosayenera ndipo kukumapangitsa kuti lamulo lisamatsatidwe. Apa nthumwi zinagwirizana kuti ntchitoyi idzigwiridwa ndi ofesi ya boma monga mkulu wowerengera ndalama za boma (Auditor Genera) ngati mmene ziliri m'madera ena.

Kachitatu nthumwi zinapempha boma kuti lifulumize kukonza magawo ena a malamulo olimbikitsira ulamuliro wabwino pothandiza kukhazikitsa malamulo moyenera.

## 9.4 Kufunika Kounika Malamulo

Anthu onse onwe anafika ku zokambirana amayamika ntchito yomwe bungwe la za malamulo limagwira mogwirizana ndi mphamvu zake. Koma anthu anadabwa ndi mchitidwe wa aphungu omwe amatsogoza zofuna zawo kusiya zofuna za anthu omwe anawasankha.

Apa anthu anali okayika ngati zomwe akupereka kuti ziphatikizidwe kapena kuchotsa pa zokambirana zowonanso malamulo ngati zingakhale za phindu popeza pamapeto pake zikaperekedwanso kwa aphungu omwewo ndipo kuti zikadutsa. Anthu ena anada nkhawa ndi kuyambitsanso lamulo loti aphungu adzitha kuchosedwa pa mpando ngati lingatheke popeza likukhudza aphungu omwewo.

## 9.5 Kayendetsedwe ka ntchito za Chuma

Imodzi mwa ndondomeko yoyendetsera chuma yomwe ikupezeka pa ndime 13 ya malamulo a boma, imayenereza boma kuti lizitha kupeza ndi kugawa chuma mofanana potsatira kayendetsedwe kabwino ka chuma.

Pazokambirana anthu ena sanakhutitsidwe ndi mfundo yokuti kayendetsedwe ka chuma kazikhala kudzera mu malamulo a dziko chifukwa chakuti boma lolamulira likhoza kukhala ndi mfundo za chuma zosiyana ndi zomwe zili m'malamulo a dziko.

## 9.6 Nyumba ya Malamulo ya Ana

Pazokambirana ndi ana ndi achinyamata, padaoneka kuti ndi kofunika kuti boma liganizireko zokhazikitsa nyumba ya malamulo ya ana mu malamulo oyendetsera dziko lino pothandiza kusula atsogoleri a mawa.